

**NJIRA ZOTETEZERA
ANA KUNKHAZA
ZOGONANA NDI
KUGWIRIRIDWA**

ZOYENERA KUDZIWA INU AUDINDO NDI ENA ONSE
OMWE ALI PA CHIOPSEZO



MAXWELL MATEWERE

NJIRA ZOTETEZERA ANA
KUNKHAZA ZOGONANA NDI
KUGWIRIRIDWA

Zoyenera kudziwa inu audindo ndi ena onse omwe ali pa
chiopsezo

MAXWELL MATEWERE

Bukuli linatsindikizidwa koyamba mchingelezi ndimutu
woti 'Betrayal of Trust' chaka cha 2016 ndi mlembi
Maxwell Matewere
Ogulitsa: M & M Publications

Copyright © Maxwell Matewere 2016

*Gawo lina lililonse la bukuli silikenyenera kutsindikizidwanso mo-
panda chilolezo chochoka kwa olemba bukuli.*

ISBN: 978-99908-0-537-6

mateweremaxwell@gmail.com

Maxwell Matewere

Box 3066

Blantyre

Malawi

MAWU OYAMBA

Bukhuli lalembedwa potsatira milandu ndi nkhanani zomwe zinachitikadi zokhudza nkhanza zogonana ndi ana komanso njira zothetsera nkhanzazi. Mayina a ana ochitiridwa nkhanzazi komanso makolo awo asinthidwa. Makolowa anadziwitsidwa za cholinga cha bukuli ndipo iwo anapereka chilolezo choti nkhanani zawo zigwiritsidwe ntchito. Milandu yonse yomwe ikukhudza nkhanani inatha ku mabwalo a milandu ndipo olakwa analandira zilango.

Ngati mlembi wa bukuli, ndikuthokoza a Malawi News Agency komanso bungwe la Lucy Foundation pa thandizo lomwe anapereka la nkhanani zina. Ndikuthokozaso mkazi wanga Whoopy Jede Matewere ndi achemwali anga, mayi Priscilla Vis, omwe ali ku dziko la America pa uphungu womwe anapereka polemba bukuli. Ndikuthokozanso bambo Kondwani Chitosi pomasulila bukukuli m'chichewa.

Pempho: bukuli likuunika mwakuya za kuyipa kwa nkhanza zogwirira ndi zogonana ndi ana ndipo likutimema kuti titengepo gawo pothetsa mchitidwe oipawu omwe ukuchitikira ana omwe alibe kuthekera koziteteza.

KUPEREKA

Ndikupereka bukuli ku mabungwe, amayi ndi makolo onse a chikondi omwe ali ndi chidwi chodziwa za mbiri zokhudza nkhanza zogwirira ndi zogonana kwa ana komanso zomwe ayenera kuchita kuti ateteze ana ku mchitidwe umenewu. Bukuli litha kugwiritsidwa ntchito ndi mabungwe, makolo komanso onse ofuna kutenga gawo pothetsa nkhanza zogonana ndi kugwirira ana m'Malawi.

MATANTHAUZO A MAUNDI ZIFUPIKITSO

CCJP: Child Care, Protection and Justice Act (CCJP)

DAC: District AIDS Coordinator

Edzi- Chipwirikiti cha matenda omwe amabwera chifukwa cha kuchepa kwa chitetezo mu thupi

HIV- Kachilombo koyambitsa matenda a Edzi

PEP- Post Exposure Prophylaxis

QECH- Queen Elizabeth Central Hospital

ZAMKATIMU

Mutu woyamba	7
Mutu wa Chiwiri	14
Mutu wa Chitatu	20
Mutu wa Chinayi	24
Mutu wa Chisanu	32
Mutu wa Chisanu	35
Mutu wa Chisanu ndi Chimodzi	49
Mutu wa Chisanu ndi Chiwiri	55
Mutu wa Chisanu ndi Chitatu	64
Mutu wa Chisanu ndi Chinayi	69
Mutu wa Chikhumi	76
Mutu wa Khumi ndi Chimodzi	80
Mutu wa Chikhumi ndi Chiwiri	90
Mutu wa Chikhumi ndi Chitatu	108

MUTUWOYAMBA

MAWUOYAMBA

Ana amakumana ndi nkhanza zosiyanasiyana. Pa chifukwa cha ichi, ndinayambitsapo ntchito zosiyana-siyana zomwe cholinga chake ndi kudziwitsa anthu za nkhanza zomwe ana amakumana nazo monga maukwati a ana, kuzembaitidwa, kuchotsedwa ziwalo komanso kugwiritsidwa ntchito zoposa msinkhu wawo. Nkhanza zambirizi zimachitika m’manyumba, m’mabanja, m’madera, m’malo opempherera, m’masukulu, malo osamalira ana a masiye, m’mindya ya tiyi ndi fodya, komanso m’malo omwe ana akugwira ntchito za m’nyumba maka m’ziminda. Bukuli likukamba za nkhanza zogonana ndi ana. Bukuli likutsindika zomwe tikuyenera kuchita kuti tipewe komanso kuteteza ana ku mchitidwe wosayenerawu womwe ukuchuluka mu dziko muno.

Kuteteza ana ku nkhanza zakuthupi komanso kupusitsidwa lidali gawo lalikulu la ntchito yanga yoteteza ana ku bungwe la Eye of the Child (2008 -2018).

Ndakhala ndikuchirimika pothetsa nkhanzazi podziwit-

sa, pophunzitsa, pochita kafukufuku komanso potengapo gawo polemba malamulo othandiza kuteteza ana ku nkhanzazi. Ntchito yanga imakhudzaso kugwira oganiziridwa, kuthandiza pozenga milandu komanso kupereka thandizo kwa ana ochitiridwa nkhanza.

Ndili okondwa ndi kusintha kwa lamulo la likulu la dziko lino la Konsititushoni, lamulo la Penal Code komanso kuyamba kugwira ntchito kwa lamulo loteteza ana la Child Care, Protection and Justice Act (2010) zomwe zakhwimitisa chitetezo cha ana komanso kupereka zilango zokhwimwa kwa ochitira nkhanza ana. Ndizachidziwikire kuti ingakhale malamulo alipo, ndipofunika kudziwitsa anthu za malamulowa.

Chofunika kwambiri ndi chakuti, makolo ndi ana akuyenera kudziwa za gawo komanso udindo wawo poteteza ufulu wa ana nthawi zonse.

Ndalemba bukuli kuti likhale chida chothandiza makolo kuti adziwe m'mene nkhanza zogonana zimachitikira komanso m'mene zimakhudzira ana. Nkhanza zogonana ndi imodzi mwa nkhanza zomwe ana amakumana nazo kwambiri ndipo zimachitika mu zikhalidwe zosiyanasiyana zomwe zimabweretsa zovuta zanthawi yayitali ku thupi ndi kumalingaliro a mwana.

Pali nkhani zambiri zomwe ana amanena zokhudza nkhanza zogonana zomwe zimasonyeza m'mene ana amamvetsetsera nkhaniza ufulu wawo komanso zomwe amaziona ngati ziphinjo pa ufulu wawo.

Nkhani yaikulu ndiyakuti m'makomo ambiri komanso anthu akuluakulu akulephera kupanga malo otetezedwa

komanso abwino oti ana adzikula mwa ufulu komanso kuti adzakhale nzika zodalirika.

Ndikudziwa kuti ntchito yopanga malo oteteza ana ili pa mtima pa boma, makolo ambiri komanso ma bungwe. Pali zambiri zomwe zikuchitika kuti ana akhale ndi moyo wa bwino pa dziko lonse. Ndongomeko ndi ntchito zambiri zakhazikitsidwa kuti zithandize kuteteza ana. Ngakhale izi zili chonchi, ana sakukhalabe mu dziko lomwe amalota. Iwo akupitirira kukhala moyo wonyozeka, ndipo choyipa kwambiri, amachitiridwa nkhanza zogonana ndi anthu omwewo omwe akuyenera kuwasamalira ndi kuwateteza.

Nkhani zambiri zokhudza ana amene akuzunzidwa zafalitsidwa. Komabe, nthawi zambiri nkhani zimenezo ziman-gosonyeza ana ngati ozunzidwa kapena ‘chiwerengero’ china.

Kawirikawiri, sitimva kuchokera kwa anawo zomwe iwo amaganiza pa nkhani zokhudza nkhanza zogonana, m’mene zimawakhudzira, ndipo koposa zonse, malingaliro awo a m’mene vutoli lingathetsedwere.

Ndazindikira kudzera mu zochitika za kusowa kwa ntchito kapena mabuku okhudzana ndi nkhanza zogonana kwa ana zomwe zimafotokoza m’mene ana achiMalawi amaonera nkhani zokhudza nkhanza zogonana ndi ana. Ndinazindiki-ra kuti nkhanza zogonana siziululidwa kawirikawiri chifukwa zimawonedwa ngati ndi zobisika mu chikhalidwe chathu.

Koma kudzera mu ntchito zofalitsa nkhani, ndaona kusintha ndipo anthu ayamba kumasuka pa nkhaniyi. Anthu akumakanena ku polisi komanso kwa ena okhudzidwa mwana akachitiridwa nkhanza zogonana.

M'maganizo a ana omwe ndachezapo nawo mu ntchito yanga andithandiza kuti ndimvetse za kukula kwa vutoli. Ana akhala akuchitiridwa nkhanzazi m'manyumba mwawo, ku sukulu komanso kumalo a ntchito.

Bukhuli lili ndi nkhani zoopsa zokhudza nkhanza zogwirira ndi zogonana kwa ana zomwe ndinazipeza pa nthawi yomwe ndimagwira ntchito yoteteza ana komanso m'mabwalo oweluzira milandu.

Mwazina, nkhanizi zikufanana kwambiri kumbali ya momwe ndinathandizira ndi kuyendetsera bwino milandu yokhudza nkhanza zogonana ndi ana; m'mene oganiziridwa milanduyi anamangidwira; komanso m'mene anazengedwera milandu ndi ku-landira zilango.

Kubweretsa chidziwitso pa nkhanizi kutha kuthandiza makolo kuti amvetse m'mene nkhanza zogwirira komaso zogonana ndi ana zimachitikira, m'mene zingapewedwere, komanso zoti achite nkhanzazi zikachitika. Owelenga athanso kudziwa zomwe angachite kuti achepetse nkhanza zogonana kwa ana.

Mubukhuli, ndaunikiranso m'mene ntchito zokhwimitsa malamulo zalepherera kuteteza ana chifukwa makolo samadziwa zoyenera kuchita ngati mwana wachitiridwa nkhanza zogonana kapena wina waonapo mwayi wopanga ndalama.

Ndili okondwa ndi nkhani zomwe anthu ochitira nkhanza ana anazengedwa milandu ndipo analandira zilango zosiyanasiyana zokhala ku ndende ndipo anawo analandira thandizo.

Ndi cholinga changa kubweretsa kusintha pa moyo wa

mwana yemwe wachitiridwa nkhanza zogonana chifukwa zotsatira za kusachitapo kanthu ngati dziko zimakhala zoo-
psa kuziganizira. Ana omwe achitiridwa nkhanza zogonana
amasiyira sukulu pa njira, amatenga matenda komanso ena
amakhala amayi nthawi yawo isanakwane.

Ndili ndi nkhanzi zomwe amayi anatengapo gawo lolim-
bikitsa kuti ana awo azigwiridwa pofuna kusunga banja
lawo. Pali milandu yambiri yomwe ana anagwiridwa ndi
abambo owapeza.

Atsikana amenewa amakamizidwa kuchotsa mimba,
nthawi zovutitsa, amagwiritsa ntchito mankhwala a zit-
samba. Ena athamangitsidwa kuti akakhale ndi agogo ku-
mudzi komwe iwo ndi ana obadwa kuchokera ku nkhanzazi
amasowa chisamaliro. Ndamvapo za nkhanzi zomwe
abambo amagwirira ana awo omwe atauzidwa ndi
asing'anga kuti ndi chizimba chopezera chuma.

Makolo ena anali ndi kuthekera koteteza ana koma
chifukwa cha kunyalanyaza anapereka mwayi woti ana awo
achitiridwe nkhanza. Iwo sanazindikire mwachangu zizind-
ikiro kapena ziopsezo ndipo ana awo anavutika kumapeto.

Palinso amayi ena omwe amachedwa kudziwitsa a polisi
komanso pali a polisi ena omwe amanyalanyaza kuchitapo
kanthu akalandira madandaulo otere posatsatira ndondome-
ko ndipo ana ochitiridwa nkhanza salandira thandizo.

Palinso atsikana ena omwe atenga matenda opatsirana
pogonana kuphatikizapo ka chilombo koyambitsa matenda
a Edzi kapena kutenga mimba, kukamizidwa kubereka
nthawi yawo isanakwane. Ena mwa iwo anayamba maten-
da a kadza mkodzo ndipo anasiyira sukulu pa njira. Dzikoli

lakhala malo opanda chitetezo kwa mwana maka mwana wa mkazi.

Mubukhuli, ndalemba nkhani zokhudza amayi komaso abambo omwe amangidwa ndi kutsekeredwa ku ndende kamba ka mchitidwe ozunza ana zomwe ndikukhulupira kuti zingameme komanso kudzetsa mkwiyo pakati pa anthu komaso makolo akufuna kwabwino kuti nkhanza zogonana ndi ana maka ana a akazi zichepe.

Ndikufuna kupanga madera athu kuti akhale malo omwe ana athu, maka a akazi, azimva kuti ndi otetezedwa komanso atha kukhulupilira anthu a akulu. Nkhani zomwe ndatolera pa nthawi yomwe ndimagwira ku mabwalo a milandu zandithandiza kukhala ndi chithunzithunzi cha nkhani ya nkhanza zogonana ndi ana pa dziko lonse. Ndayika nkhanizi ngati njira yobweretsa chidwi komanso kumema anthu kuti athetse nkhanza zonse zogonana ndi ana.

Nkhanizi zikuonetsa kuvunda kwa amayi, abambo ndi makolo ena m'madera athu. Cholinga chachikulu ndikudziwitsa anthu za vuto lalikulu la nkhanza zogonana zomwe ana amakumana nazo komanso kudziwitsa makolo za zizindikiro za chiopsezo komanso kuti azichitapo kanthu mwachangu kuti apewe nkhanza za mtundu uliwonse. Ndikufuna ndione makolo komanso osamalira ana akukhala ndi chikhalidwe cholemekeza lamulo loteteza ana la Child Care, Protection and Justice Act- (2010).

Tonse tikumbutsidwe kuti tili ndi udindo woteteza ufulu wa ana ndipo tipange malo omwe angalole ana kuti akule ndikukhala anthu a chikondi omwe adzathe kusamalira ana awo. Tikumbukirenso kuti zomwe zimachitikira ana lero zidzakhudza momwe adzasamalire ana awo.

MUTU WA CHIWIRI

KUBWALOLA MLANDU

Ulendo wanthu ukuyamba ndikupita kubwalo loweluza milandu. Mabwalo oweluza milandu akuyenera kupereka zilango zokhwima kwambiri kwa aliyense wopezeka akuzunza ana. Tsiku lina, ndimkalingalila za kufunika kwa zilango zokhwimazi pa nthawi yomwe ndinali ku bwalo loweluza milandu ya Lilongwe Magistrate. Ndinapita ku bwalo loweluza milanduli kukatsatira mulandu womwe bambo anachitira nkhanza zogwirira mtsikana.

Zolemba zikuonetsa kuti mwana wochitiridwa nkhanzayu anali ndizaka zomwe malamulo samalola kuti atha kuvomera kuchita zogonana. Iye anali ndi zaka 13 zakubadwa pa nthawi yomwe nkhanzayi inachitika. Iye anagwiriridwa mwezi wa Febuluwale mu chaka cha 2015 ku Chilinde mu mzinda wa Lilongwe mu dziko la Malawi. Wogwirira anali bambo wa zaka 44 za kubadwa. Zinadziwika kuti anamupatsa pakati kapena titi mimba.

Bamboyu anali munthu yemwe mwanayu amamukhulupirira. Bamboyu ndi mkazi wake, yemwensu analinso ndi

mimba pa nthawi yomwe mulandu umazengedwa, amkasamalira mwanayo yemwe ndi wa masiye. Mayi a mwanayu anali malemu mchemwali wa mkazi wa bamboyu. M'malo molera mwanayu, bamboyu adapezerapo mwayi wochitira nkhanza mwanayu.

Ndinali okondwa kwambiri nditaona kuti bwalo loweluza milanduli linaunikira zovuta zomwe mwanayu anakumana nazo pa nthawi yomwe anali woyembekezera komanso pobereka potengera kuti mwana wa zaka 13 zakubadwa amakhala wosakhwima. Kubereka ndi chiopsezo chapamoyo chomwe mzimayi wokhwima nsinkhu amayenera kuvomereza mosakakamizidwa.

Ndikukumbukira bwino tsiku lina ndikumvetsera mulandu ku bwalo loweruza milandu la Lilongwe Magistrate, ndinalandira uthenga pa foni yanga ya m'manja.

Uthengawu unati: “Bwalo loweluza milandu laling'ono ku Machinga lapeza a Madalitso Simbwani a zaka 42 zakubadwa olakwa pa mulandu wochita za mathanyula ndi mwana wamamuna wa zaka 11 zakubadwa ndipo lalamula kuti akakhale ku ndende kwa zaka 12.”

A Simbwani anavomera mulanduwo womwe umasutsana ndi gawo 153 la lamulo la Malawi Penal Code.

Mlandu wa a Simbwani usanayambe, kafukufuku waku chipatala cha boma la Machinga anaonetsa kuti mwanayu anachitidwadi mathanyula. Mwanayu anavulala pomwe amamukakamiza kuchita mathanyula.

Nthawi yomva mulanduwo, a Sub Inspector Ezekiel Kalunga omwe a polisi omwe adatengera mulanduwo kubwalo loweruza milandu, anauza bwalo la milandu kuti a Simb-

wani anatengera mwanayu ku nyumba yomwe imamangidwa ku tawuni ya Liwonde komwe anakamuchita nkhanzazo.

Wozenga mulanduwu anafotokozanso kuti mwanayu anapulumitsidwa ndi anthu omwe amadutsa omwe anamumva akukuwa. “Mnyamatayu analinso akusanza kutsatira kugonedwa mkamwa mokakamizidwa ndi a Simbwani,” a Sub Inspector Kalunga anafotokozerabwalo loweluza milandu.

Oweluza milanduwu, a First Grade Magistrate Esther Phiri, anadzudzula kwambiri zomwe zinachitikazi. Oweluza milanduyu anati a Simbwani akuyenera kulandira chilango chokhwima kwambiri ndi chifukwa chake anagamula kuti akakhale ku ndende kwa zaka 12.

A Simbwani amachokera m’ mudzi mwa Lenadi mude-ra la mfumu yayikulu Sitola m’boma la Machinga. Mwana wochitiridwa nkhanzayu anali mwana wongoyendayenda pa tawuni ya Liwonde.

Akaswiri a za umoyo amaletsa mchitidwe wa mathanyula. Woyendetsa ntchito za matenda a Edzi m’boma la Machingaga (District Aids Coordinator- DAC), a Ben Tohno, anati mchitidwe wa mathanyula umafalitsa kwambiri ka chilombo koyambitsa matenda a Edzi. A Tohno anafotokoza kuti ka chilomboka kamadutsa mosavutikira m’ mabala omwe amabwera pochita mathanyula.

A Tihno anapemphanso anthu kuti azitengera onse ochitidwa nkhanza zamathanyula, zogonana ndi mwana komanso zogwirira ku chipatala chomwe chili pafupi kuti akawayeze ngati ali ndi ka chilombo koyambitsa matenda a Edzi. Iwo anati, ngati kuli kofunika, wochitiridwa nkhanzayo amakalandira mankhwala a PEP omwe amaletsa ka chilombo

koyambitsa matenda a Edzi kuti kakhazikike.

Mankhwala a PEP ali mu gulu la mankhwala otalikit-sa moyo omwe amapatsidwa kwa anthu omwe achitiridwa nkhanza zogonana kapena omwe akuganizira kuti apatsidwa ka chilombo koyambitsa matenda a Edzi mwangozi. Mankhwala amayenera kuyamba kumwedwa pasanathe maola 72 kuchokera pomwe zinthu zoika chiopsezo zachitika.

Ndiloleni ndibwerere ku mulandu waku Lilongwe uja. Pamene woweluzana milandu amapereka chigamulo chake, ndikukumbukira kuti wozengedwa mulandu sanavomere mulandu. Ndili ndi chikhulupiriro kuti izi zinachepetsa mwayi wake wolandira chilango chopepuka.

Iye amayenera kukakhala ku ndende kwa nthawi ya itali komwe akagwire ntchito ya kalavula gaga potayitsa nthawi ya bwalo la milandu, mboni, komanso aliyense pomva mulandu womwe iye akanatha kuwuvomera pa chiyambi. Pa mulandu uliwonse, ndi mfundo ya lamulo imati, kuvomera mulandu kumakhala chinthu chimodzi chomwe chimayenera kuchiganizira popereka chilango kapena popeza njira zina zothetsera mulandu.

Ndikukumbukiranso kuti wozengedwa mulanduyu amkavuta pa nthawi yomwe mulandu umazengedwa. Nthawi zina amabweretsa mboni zake mosadziwitsa ogwira ntchito ku bwalo la milandu. Nthawi ina, anadzetsa chisokonezo pamene amkafuna kuthawa unyolo uli m'manja ku bwalo loweluzana milandu.

Poziteteza, iye anati mulanduwu unali waung'ono ndipo banja lake likanatha kuthana nawo mosavuta.

Tinakhala kwa nthawi yopitirira ola limodzi kumvetsera chigamulo cha mulandu.

“Woganiziridwa mulandu anazengedwa komanso kugamulidwa potengera gawo 138(1) la lamulo la Penal Code. Olakwa mulandu amayenera kulandira chilango chokhala ku ndende ndi kugwira ntchito ya kalavula gaga kwa moyo wonse,” anafotokoza woweluzi mulandu ku bwalo la Chief Resident Magistrate.

Oweluzi mulandu anati: “Popereka chigamulo bwalo loweluzi mulandu launikira zinthu zokulitsa komanso zochepetsera mulandu lisanafike popereka chilango choyenera.”

Iwo anapitiriza kuti: “Nthawi zonse, izi zimakhudza kuona mulingo womwe mulandu unachitikira, umoyo wa ochitiridwa nkhanza, m’mene upandu wamukhudzira wochitiridwa nkhanza, komanso chidwi cha anthu pofuna kupewa milanduyi”.

Pamene woweluzi mulandu amawerenga chigamulo, ndinatembenuka ndikuyang’ana ochitiridwa nkhanzayo. Ndinalingalira kuti maphunziro ake anali atasokonekera. Pa nthawiyo anali mu Sitandade 7.

Iye akuyenera kugonjetsa manyazi ndi kulefulidwa komwe kungakhalepo pa nthawi yomwe iye adzafune kubwerera ku sukulu akadzabereka. Ndi chikhulupiriro changa kuti iye adzalimba mtima kuti akonze tsogolo lake ingakhale ali ndi ziphinjo zambiri. Maganizowa anandikumbutsa za nkhani ya Bessie, mtsikana waku Ndirande mu mzinda wa Blantyre.

MUTU WA CHITATU

MTSIKANA BESSIE

Inali ngati tsiku lililonso lomwe Bessie amasewera ndi anzake panja pa nyumba ya makolo ake. Zinthu zinasintha mwadzidzidzi kwa mtsikana wa zaka 11 zakubadwayu.

Chigawenga china chodziwika bwino muderalo chotchedwa Jarvis chidatulukira mwa dzidzidzi pa malopo. Jarvis sananene kanthu. Iye anangoloza chala kwa Bessie ndikumuwuza kuti amutsatire.

Anzake a Bessie anamulangiza kuti atsatire chigawengacho chifukwa iwo amaganiza kuti kusamvera kutha kubweretsa mavuto ena pa iye.

Bessie anamveradi amzakewo ndikutsatira bamboyo. Bessie akunyamuka ndi chigawengacho, amzake anakawauza mayi ake zomwe Jarvis wachita.

Jarvis anamutengera Bessie ku nyumba kwake. Kumeneko anamuuzza Bessie kuti iwo ndi banja tsopano. Bessie analira koma bamboyo anamukhazika chete. Anamugwiririra kangapo. Jarvis anamuopseza Bessie kuti athana naye akay-

erekeza kuthawa ku banjako.

“Aka kanali koyamba kuti ndichite zogonana. Zinali zopweta kwambiri. Ululuwo unandiganizitsa zoti ndingofa. Ndikamalira, bamboyo amkanditseka pa kamwa. Iye amkandivula kenaka kundigwiririra.” Bessie anapitiriza kufotokoza;

“Kwa masiku awiri, ndinagona pa bedi lake mu ululu. Iye amkabweretsa zakudya koma ndinakanika kudya. Nthawi zonse ndikayesera kudya, ndi mkasanza. Khumbo langa linali loti makolo anga andipulumutse. Koma makolo anga kapena wa chifundo sanabwere kudzandipulumutsa. Jarvis anasiya kundigwirira ataona kuti ndimatuluka magazi ku maliseche. Chilombochi chinati kutuluka magaziko chinali chizindikiro chakuti ndilino wokonzeka kuyamba banja. Iye anati ndinali woyenera kukhala mkazi wake poti ndinali ndisanagonepo ndi munthu.”

Mayi ake a Bessie, Anaphiri, anamusaka mwana wawo ndipo anamupeza ku nyumba kwa bamboyo. Iwo anayesera kukambirana ndi Jarvis kuti amusiye Bessie koma iye anakanisitsa.

“Gogo iwe, yu ndi mkazi wanga ndipo ukayerekeza kuwuzza anthu za banjali, uona mkwiyo wanga,” Jarvis anaopseza.

Anaphiri sanalimbane naye ndipo anapita kwao okhumudwa. Iwo ali ndi ana anayi. Amuna awo anali ku ndende komwe analowa atapezeka olakwa pa milandu yakuba.

Bessie anakhala ndi Jarvis kwa ma sabata awiri. Pa nthawi yonseyi, Jarvis sanamulole kuti atuluke munyumba. Iyenso sanachoke.

Anaphiri anapempha atsogoleri amuderalo kuti awathan-

dize kupulumutsa Bessie. Zinaoneka kuti panalibe yemwe analimba mtima kuti achitepo kanthu.

Ndinadziwa za nkhaniyi pomwe munthu wina wokhala ku Ndirande anadzatula nkhaniyi ku ofesi kwanga.

Ndinayamba kafukufuku pa nkhaniyi. Kafukufuku wanga anasonyeza kuti Jarvis analidi chigawenga chodziwika bwino. Izi zinatanthauza kuti kunali koopsa kuti ndipiteko ndekha. Apa ndi pomwe ndinapita kukapeza thandizo ku polisi.

Apolisi anazindikira kuti bamboyo amafunidwa pa milan-du yosiyanasiyana. Iwo anamumanga atathyola chitseko cha nyumbayo ndikumupulumutsa mtsikanayo. Iwo anamutseg-ulira milandu iwiri, wogona ndi mwana komanso wokuba mwana.

“Sindikudziwa chomwe mukufuna kundimangira pomwe ine ndachita zomwe mamuna aliyense amachita. Ndinamukwatira Bessie. Timachita zomwe mamuna ndi mkazi amachita m’banja. Iye simwana. Ingakhale mayi ake akudziwa kuti iye sanali mwana pa nthawi yomwe ndimamukwatira. Ndi chikhalidwe chathu kukwatira ana. Makolo ake anavomereza ukwatiwu,” Jarvis anauza bwalo la milandu.

Zinali zoopsa kuona bamboyo akuvomera kuti anatenga Bessie, mwana wa zaka 11 zakubadwa, kukhala mkazi wake. Iye sanaonetse chisoni ndipo anauza bwalo la milandu kuti wakonzeka kumangitsa banjalo kuti likhale lovomerezeka.

Bwalo la milandu linamupeza Jarvis wolakwa pa milandu wogwiririra komanso wokuba mwana ndipo inalamula kuti akakhale ku ndende kwa zaka 12.

Ndinamutumiza Bessie ku sukulu ndipo bungwe langa likuthandiza banja la kwawo. Ndili ndi chikhulupiro chokuti

thandizo lomwe Bessie akulandira lizamuthandiza kukha-lan
ndi moyo wa bwino ingakhale anapatsidwa ka chilombo
koyambitsa matenda a Edzi.

MUTU WA CHINAYI

MALAMULO

Mu gawo ili, ndiyamba ndi kufotokoza tanthauzo la nkhanza zogonana kuno ku Malawi mogwirizana ndi malamulo a dziko lino. Ndagwiritsa ntchito mawu angapo pofotokoza mitundu yosiyanasiyana ya nkhanza zogonana m’magawo omwe ali mbuyomu. Ndiloleni tso-pano kuti ndifotokoze matanthauzo a mauwa.

Mlandu woyamba ndi mlandu wokhudza Kugonana ndi mwana wa mkazi: Uwu ndi mtundu wa nkhanza zogonana zomwe zimachitika pomwe munthu wagonana ndi mwana wa mkazi yemwe sanakwanitse zaka 18 zakubadwa ku Malawi.

Gawo 138 (1) la lamulo la Penal Code (Cap 7:01) limati:

“Aliyense amene agone ndi msungwana wosakwanitsa zaka 18 zakubadwa adzakhalala wopalamula ndipo adzakhalala m’ndende moyo wonse.”

Zatsindikidwa kuti munthu amapalamula mulanduwo posatengera kuti mwanayo anavomera kapena ayi, kusonyeza

kuti chilolezo cha mwana ndi chosatheka.

Kugonana ndi mwana wa mkazi kumatanthauza kuti chiwalo cha umuna cha abambo chalowa ku chiwalo cha ukazi cha mwana wa mkazi. Umboni woti ku chiwalo cha ukazi cha mwanayo kunalowadi chiwalo cha umuna ndi ofunika kwambiri potsimikiza mlanduwu. Mlanduwu umapalamulidwa kwambiri ndi abambo omwe amapatsidwa udindo wosamalira ana.

Nthawi zambiri, mwana amavulala kwambiri akachitidwa nkhanza ya mtunduwu.

Mlandu wachiwiri ndi mlandu okhudza mochita zogonana ndi mwana: Mlandu uwu unabweretsedwa posachedwa pamene malamulo amakonzedwanso. Mlanduwu umachitika pomwe munthu wachita zinthu zogonana ndi mwana wa m'muna kapena wa mkazi ndipo pamangofunika umboni woti munthuyo anagwira ziwalo zobisika kapena mabere a mwanayo kapena anamukakamiza mwanayo kuti agwire maliseche a munthu wa mkulu.

Gawo 160 A la lamulo la Penal Code limafotokoza mlanduwu motere: *“Kugonana kwina kosakhuza kulowetsa chiwalo cha umuna ku chachikazi... monga kuyika chiwalo cha umuna kukamwa kapena ku matako; kuseweretsa maliseche; kugwirana maliseche, matako kapena mabere; kuzunza munthu wina m'thupi kapena m'maganizo pofuna kudzutsa chisangalalo cha kugonana ndi chisangalalo; ndi zonyansa zina zogonana.”*

Ndipo gawo 160 B la lamulo la Penal Code limati:

“Munthu aliyense amene achita zogonana ndi mwana [wa zaka zosakwana 18 zakhadwa] adzakhalala wolakwa ndipo adzakhalala kundende zaka khumi ndi zinayi.”

Ngati mulanduwu wachitika poopseza (monga kumuopseza mwanayo, kukhala kholo lomupeza kapena womulera, kape-na mphunzitsi), wolakwayo adzakhala ku ndende kwa zaka 21.

Mlandu wachitatatu ukukhudza Nkhanza zogonana kudzela kuzoonetsa, kutola zithunzi ndi kugulitsa, kapenaso kumusonyeza mwana zithuzi zolaula: Anthu ambiri amavutika kumvesetsa za mulandu wa nkhanza zogonana makamaka ngati zikukhudza zinthu za ukadaulo pa kuyezetsa ku chipatala komanso mumabwalo a milandu. Pali matathandauzo ambiri a nkhanza zogonana.

Mubukuli, ndikuona thandauzo la nkhanza zogonana kwa mwana motengera malamulo a dziko la Malawi.

Nkhanzazi zimachitika mu njira zosiyanasiyana komanso zimatha kuchitidwa ndi mwana wa mkuluko kuyerekeza ndi wochitiridwayo.

Nkhanza zogonana, mwachitsanzo, zimachitika pomwe munthu wamugwira mwana mu njira yomwe mwanayo sanasangalale nako kapena kumupatsa mantha.

Njira ina imachitika pomwe munthu wamukakamiza mwana kuti amugwire. Nthawi zina, munthu wamkulu amatha kumuwuzwa mwana kuti avule zovala. Pa nthawi imeneyi, munthu wa mkulu amaonetsa maliseche ake kwa mwanayo.

Ana amaonetsedwanso kapena amagwiritsidwa ntchito powonera zolaula.

Zolaula zikutanthauza kugwiritsa ntchito zithunzi, kane-ma a maliseche kapena ogonana.

Ndikoyenera kuzindikira kuti wina aliyense yemwe an-

galole mwana kuti aone kapena aonere zolaula wapalamula mulandu wochita nkhanza zogonana wotchedwa ‘kuonet-sa, kugulitsa kapena kusonyeza zinthu zokhumudwitsa kwa mwana’ malingana ndi gawo 160 D la lamulo la Penal Code ndipo adzakhala ku ndende kwa zaka zisanu ndi ziwiri.

M’madera mwathu mwachitika milandu yambiri ya nkhan-za ndipo ndikofunika kwambiri kuti anthu ambiri adziwe za nkhanizi kuti pakhale kusintha.

Chomwe chikudziwika ndi chakuti nkhanzazi zimachitika nthawi ina iliyonse komanso kwina kulikonse. Pa chifukwa ichi, ndikofunika kwambiri kuti ana aphunzire momwe angazitetezere ndipo makolo ali ndi udindo wopewetsa nkhan-za. Makolo ayesetse kuphunzitsa ana za mitundu ya nkhanza.

Mlandu wachinayi ukukhudza uhule wa ana kapena kugwiritsa ntchito ana pa malonda a uhule: Izi zikuphatikizapo mchitidwe wogwiritsa ntchito ana kuti agone nawo posinthanitsa ndi ndalama kapena mphotho ina iliyonse. Mwanayo amatengedwa ngati chinthu chogonana nacho komanso malonda. Uwu ndi mulandu pa gawo 160 E la lamulo la Penal Code.

Zimenezi zimachitika m’malo olinganizidwa bwino monga nyumba zosungiramo mahule, kapena pamene makolo kapena olera ana achititsa anawo uhule ku nyumba kapena m’makwalala pofuna kusinthanitsa ndi ndalama kapena zinthu zina.

Ana ena amachitiridwa nkhanzazi ku sukulu, m’malo okwerera galimoto zapaulendo monga matakisi ndi mabasi, m’magulu achifwamba kapena m’malo omwera mowa. Ana amenewa amachitidwa nkhanza zogonana ndipo nthawi

zambiri amagwiridwa kangapo pa tsiku. Nthawi zina amamenyedwa ndikuwopsezewa kuti aphedwa ngati ataulule za nkhanzazi kwa aliyense.

Anawa amakakamizidwa kuti agwiritse ntchito mankhwa-la osokoneza ubongo kuti athetse ululu umene umabwera chifukwa cha kugwiridwa. Anawa amaonetsedwanso za upandu zazikulu, monga kuthyola magalimoto ndi kuba.

Mlandu wachisanu ndi chimodzi umakhudza Kugonana pa chibale: Zodabwitsa kwambiri ndi nkhanzi za abambo kapena abambo owapeza kapena amalume akugonana ndi ana awo, mphwawo, kapena adzukulu awo. Kugonana pa chibale kumachitika pakati pa achibale omwe amalisedwa kutero monga omwe ubale wawo uli pa magazi, ukwati, kapena polerana, monga kugonana kwa abambo ndi mwana wake wa mkazi kapena amayi ndi mwana wake wa mwamuna.

Malinga ndi malipoti a ofalitsa nkhanzi komanso kafukufuku wa omenyera ufulu wa ana osiyanasiyana, pali milandu yambiri ya achibale omwe amachitira nkhanza atsikana m'nyumba chifukwa cha kufooka komanso kusatetezeka kwa ana ambiri, m'mabanja angapo, milandu yoteroyo siyimanenezedwa.

Pali zinthu zingapo zomwe zimapangitsa kuti milandu yogonana ndi wachibale isamanenezedwe kwambiri. Chifukwa cha banja lake, mayi amasankha kusunga chinsinsi chokuti mwamuna wake amagona ndi mwana wawo wa mkazi. Mlongo sangayerekeze kuulula kuti achimwene ake omupeza amamugona.

Kugwiridwa malo osayenera ndi kuzuzidwa mogonana

ndi mitundu ina ya nkhanza zogonana ndi mwana.

Mlandu wachisanu ndi chitatu umakhudza Kugwiridwa malo osayenera: kugwiridwa malo osayenera kumachitika mu njira zosiyanasiyana. Mulanduwu umapezeka mu gawo 137 ya lamulo la Penal Code. Kulowetsa chinthu monga botolo kapena nthochi ku maliseche kwa mwana wa mkazi kapena kumbuyo kwa mwana wa m'muna ndi mulandu wogwira malo osayenera. Kukakamiza munthu kuti agwire kapena ayamwe maliseche ndi mulandu wogwira malo osayenera. Bambo yemwe alowetsa chiwalo chake cha umuna ku mbuyo kwa munthu wina amakhalanso kuti wapalamula mulanduwu.

Kuchitidwa chipongwe mwa kugonana: Uku kumachitika, malingana ndi gawo 6 la lamulo losawona kusiyana pakati pa akazi ndi amuna (Gender Equality Act), pomwe wina aonetsa zizindikiro zosonyeza zogonana kwa mwana. Izi zikapitirira ndipo mwanayo wanyasidwa nazo mwachidziwikire, ndekuti mulandowo wachitika.

Kuchitidwa chipongwe mwa kugonana kumapangitsa ana kuti asemphane ndi mwayi wa maphunziro zomwe zimasonkoneza tsogolo lawo. Ana amatetezedwa pomwe makolo komanso anthu okhala moyandikana nawo akukhala tcheru pa mchitidwewu.

Milandu yambiri ya nkhanza zogonana yomwe tatchulayi imachitika ku Malawi.

Kuthetsa mchitidwe wopalamula milandu yotero kwakhala kovuta kwambiri chifukwa cha zikhulupiriro za chikhalidwe kapena chikhalidwe cha olakwa.

Ana samadziwitsidwa za mitundu yambiri ya nkhanza

zogonana ndi momwe angapewere chifukwa chakuti makolo samamasuka mokwanira pokamba nkhani zogonana. Izi zimapangitsa kuti anthu a upandu asavutike kuwachita nkhanza anawa.

Chifukwa cha nkhabakamwa yokhudzana ndi kugonana, ana amayesa pa iwo okha kuti athane ndi mavuto omwe akumana nawo ndipo nthawi zambiri zotsatira zake zimakhala zopweteka kwambiri.

Ana amene akumana ndi nkhanza zogonana mwa njira zosiyanasiyana amakula akukhulupirira kuti palibe cholakwa kuchitira nkhanza zogonana kwa anzawo. Kafukufuku amasonyeza kuti anthu ambiri omwe amapalamula milandu yogwiririra amakhala kuti anachitidwa nkhanza zogonana ali ana.

Ndimayesetsa kudziwitsa anthu za kuopsa kochita nkhanza zogonana. Mwayi ukapezeka, ndimakambirana ndi makolo za m'mene angapewere vutoli. Ndakumanapo ndi milandu yomwe makolo eniwo ndi amene akhala akuchita nkhanza zogonana. Ndamva nkhani za makolo amene anagonana ndi ana awo omwe potsatira malangizo a asing'anga.

Akuti 'asing'anga' amenewa amapereka malangizo oterowo kwa anthu amene akufunitsitsa kupeza chuma osachigwirira ntchito. Nthawi zambiri, mtsikana ndi amene amachitiridwa nkhanza pa nkhani zimenezi.

Palinso nkhani za abambo omwe amalangizidwa kuti agone ndi ana awo a akazi a ang'ono ngati akufuna kuchiritsidwa ku matenda osiyanasiyana, kuphatikizapo matenda opatsirana pogonana.

MUTUWA CHISANU

MAGANIZO A ANA

Kuti ndimvetse bwino nkhaniyi, ndinakambirana ndi ophunzira a sukulu za pulayimale za Nyambadwe, Chichiri, Chitsime, Chitawira, ndi H.H.I. mu boma la Blantyre.

Ndinagwiranso ntchito ndi ophunzira ku sukulu za Our Lady of Wisdom, Chisomo Children's Club, Ndirande Hill Secondary School ku Blantyre ndi Chathope Community Day Secondary School (CDSS) ku Kasungu polemba zomwe akudziwa zokhudza nkhanza zochitika pogonana.

Ndinawalola kuti afotokoze maganizo awo kudzera muzolemba za luso. Ntchito imene anatulutsa imasonyeza kuti anawo amamvetsa zavutoli. Koma chowatchinga chachikulu pothana ndi mavutowa ndi chakuti alibe mphamvu pamaso pa m'dani wa mkulu. Awa ndi anthu a akulu omwe amapezerapo mwayi pa ana komanso kufooka kwa zokhwimitsa malamulo kuti apitirize kuchita zinthu komanso makhalidwe osayenera omwe amaika moyo wa mwanayo pa chiswe.

“...Ana ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. Choncho, ndi pofunika kuti aliyense azikonda mphatsoyo m’njira yabwino kwambiri.”

Hassan Lyson

Ndizachidziwikire kuti akuluakulu amamvetsetsa kuti ana ndi mphatso yochokera kwa Mulungu koma mukamawerenga kapena kumva nkhanzi za nkhanza zomwe akuchitira mphatso imeneyi, mumadabwa ngati anthu amayamikiradi kuti ali ndi mphatso mwa mwana aliyense. Makolo ena amayamikira mphatsoyo ndipo amasalira ana awo munjira yoyenera. Koma pali ena ambiri kunjira uko amene amachitira nkhanza mphatso imeneyi.

“...Ana ambiri amachitiridwa nkhanza chifukwa makolo ena makamaka abambo amathawa udindo wosalira ma banja awo, kusiyi izi m’manja mwa akazi awo amene sangakanitse kusamalira ana awo.”

Ackim Kamwaza, Nyambadwe Primary School

Ndinakumana ndi makolo amene amaoneka kuti alibe chidwi pa udindo wawo pa ana awo. Palinso ena amene amakonda kuti ana awo azisamaliridwa ndi anthu ena pamene iwo amatanganidwa ndi zinthu zina. Anawo amazindikira izi, koma amakhala ofooka, amangoyang’ana mopanda chiyembekezo pamene akuvutika mwakachetechete.

Uthenga womwe uli pansipa ndi umodzi mwa kulira ndi zokhumba zambiri kochokera kwa ana omwe akukumana ndi ululu wa kunyalanyaza:

Ndakatululo ndi uthenga kwa Ozunza ana:

Ulendo Wathu Ulendo wathu wangoyamba

kumene

Kuti tikwaniritse

Koma popanda nkhwawa kapena chisamaliro

Chigawengacho chimatilanda zonse zomwe tinali nazo

Pali dziko langwiro

Pa tsogolo pathupa

Kumene ana ali omasuka kukhala zonse zomwe

angathe Koma inu mwadula njira yawo

Pali zambiri zoti tichite kuposa zomwe tingathe kuchita

Zambiri zopezeka kuposa zomwe sizingabwenzeretsedwe

Koma mumachotsa zomwe sizingasinthidwe

Pamene mukukwaniritsa zokhumba

Tsopano ndi nthawi yanu kuti mukumane

nazo Ndi nthawi yoti mukumane nazo

Zowawa ndi mazunzo zomwe mudandiyikamo

Zabweranso kudzakuvutitsani

Caron S. Magombo, Our Lady of Wisdom, Blantyre

MUTUWA CHISANU

KUCHIPATALA

Pamene ndimayendetsa nkhani ya Bessie, ndidaitanidwanso kuti ndikatsatire nkhani ya Maureen wa zaka 17 zakubadwa yemwe amakhala mu mzinda wa Blantyre. Iye anakumana ndi nkhanza m'manja mwa mchimwene wake womupeza.

Maureen anali folomu folo pa sukulu ina ya sekondale mu mzindawu. Mayi ake anakwatiwanso bambo ake atamwalira. Mwamuna wa tsopanoyo adabwera ndi mwana wa mamuna wa zaka 21 zakubadwa yemwe amaphunzira ku koleji ina mu mzindawu.

Mchimwene wake womupezayo adafuna kugonana kangapo ndi Maureen koma adakana. Maureen adakafotokozera mayi ake za nkhaniyi koma sanamvere dandaulo lake. Mnyamatayo anapitiriza kuyesera kumukakamiza kuti agone nayebe koma Maureen amakanisitsabe.

Usiku wina, mnyamatayo anaika mankhwala mu chakumwa cha Maureen atangomaliza kudya chakudya cha madzulo. Maureen anagona tulo tofa nato ndipo mchimwene wake

womupezayo anamugwiririra. M'mawâ mwake anazindikira kuti wagwiriridwa. Mtsikanayo anauza mayi ake za vutolo. Apanso amayi sankhulupilire nkhaniyi. Mayiwo anamukalipira ponena kuti iye ndi amene anamuitana mchimwene wakeyo ku chipinda kwake.

Maureen adafotokoza nkhaniyi kwa anzake. M'modzi mwa iwo adamulangiza kuti apite ku One Stop Centre yaku chipatala cha Queen Elizabeth Central (QECH) yomwe imathandiza anthu omwe akukumana ndi nkhanza zogonana komanso kupereka uphungu kwa anthu omwe akhudzidwawo mwa zina.

Anapita kumeneko maola 72 asanadutse chigwiriridwireni. Analandira mankhwala a Post Exposure Prophylaxis (PEP) omwe amateteza munthu kuti asatenge matenda opatsirana pogonana komanso ka chilombo koyambitsa matenda a Edzi. Analandiranso mankhwala oletsa kutenga pakati. Iye anapatsidwa uphungu komabe iye anakhalabe ndi nkhwawa. Iye anapemphanso thandizo ku maofesi athu.

Ndinaona kuti mlanduwu unali waukulu kwambiri. Ndinazindikiranso kuti ngati nkhaniyi siyiyendetsedwa mosamala, kugwiriridwako kutha kupitirira ndipo mapeto ake zifika povuta kwambiri. Ndinakumana ndi makolo ake onse awiri omwe poyamba sanafune kumva zomwe ndimafotokoza. Koma patapita nthawi yaitali ndikuwapatsa uphungu, anamvetsa m'mene zinthu zinalili.

Ndinakwanitsa kulekanitsa anawo potengera Maureen ku sukulu yogonera. Mnyamata nayenso anapatsidwa uphungu.

Ndinakwanitsanso kumuzindikiritisa mnyamatayo kuti walakwa kwambiri. Iye anali ndi mwayi. Iye anapulumuka

potengera kuti panalibe umboni wa chindunji wotsimikiza kuti iye ndi amene anagwiririra Maureen malingana ndi ufyfuza milandu ku Polisi. Umboni wokwanira ukanakhalapo a Polisi akanachita zoyenera pa nthawi yomwe anadziwa za nkhanayi.

Mlanduwu udawulula gawo lomwe nthawi zambiri silimalabadiridwa mu ndondomeko zathu; nkhanza za m'nyumba. Izi zikapanda kusamaliridwa bwino, zitha kukhala ndi zotsatira zoyipa.

Ngakhale kuti Maureen ali ku sukulu yogonera, ubale wake ndi mchimwene wakeyo udakali wovuta ndipo banjalo lilibe mtendere. Mavuto akudza chifukwa cha nkhasoyo. Ndidapitiriza kupereka uphungu ku banjali koma mtendere weniweni sunakhalepo pokhapokha ngati mbali zonse zingakhale zofunitsitsa komanso zokonzeka ku-vomereza zomwe zinachitika ndi kupita chitsogolo.

Maureen adaulula kwa mlangizi wathu kuti amalakalaka mayi ake atasudzulana ndi bambo womupezayo chifukwa amawatenga ngati ndi omwe adayambitsa vutoli pobweretsa mwana wawo m'nyumba mwawo. Ngakhale kuti bamboyo amayesa kumuchitira zabwino, Maureen samagwirizanebe naye.

Pantchito yanga, ndanakhala ndikulandira milandu yambiri yofanana ndi umenewu. Ndazindikira kuti m'mabanja omwe makolo adasudzulana ndi kukwatiranso amakhala ndi mikangano yobwera chifukwa cha nkhanza zogonana.

Magulu awiri a anawa nthawi zambiri samadzimva kuti ndi anthu a m'banja limodzi, ndipo ndizoletsedwa pa chikhalidwe komanso pa malamulo kuchita zibwenzi zogonana. Ndi udindo wa makolo kuphunzitsa ana awo chifukwa chimene ayenera kukhalira ngati abale.

Maureen akuchirabe chifukwa cha ululu wa maganizo ndi wakuthupi umene anakumana nawo. Anasamuka ku nyumba kwa amayi ake ndipo amakhala ndi azakhali ake.

Ubale wake ndi amayi ake sulinso bwino. Koma ndinayesera kuwayanjanitsa powapatsa uphungu limodzi.

Ingakhale ntchitozi zikubala zipatso, ululu wogwiriridwa ndi m'bale wake weniweni umamupwetekabe. Iye anaulula kuti amalota zoopsa ndipo akhoza kukhala ndi moyo wo-sakhululukira mchimwene wake womupezayo.

Milandu ina yogwiririra yomwe imafika ku ofesi yanga imakhala yochitidwa ndi achibale kapena okhala nawo moy-andikana. Izi zimachitika nthawi zonse. Nthawi zambiri ana amachitidwa nkhanza ndi anthu omwe amawadziwa. Makolo ena amasankha kukhala chete, pamene ena amapita kwa adindo oyenelera.

Anthu amakhulupirira kwambiri bungwe langa moti ndi-malandira milandu yambiri ya atsikana amene amagwiriridwa. Ndimagwira ntchito limodzi ndi akuluakulu a boma kuti atsekere olakwa. Milandu yambiri imachokera kwa anthu omwe amadziwana ndi atsikana monga okhala nawo moyandikana ndipo nthawi zina achibale awo.

Kuti ndithe kuthandiza pa milanduyi, nthawi zambiri ndimadalira mgwirizano wathu ndi a zaumoyo komanso akuluakulu a za malamulo omwe ayenera kupereka umboni wofunikira kuti milandu yotereyi ipite ku bwalo la milandu.

Nthawi zina ndimakhala ndi mavuto pamene umboni wofunikira ukusowa kapena pamene pali kusafuna kupereka umboni. Zimakhala zovuta kutengera nkhani zotere kukhoti ndi kupeza chithandizo kwa ochitiridwa nkhanza.

Mavuto a Nachisale

Chitsanzo chabwino ndi cha Nachisale waku Ndirande. Nachisale anabadwa wopanda chilema ngati mwana wina aliyense. Iye anayamba sitandade 1 ali ndi zaka zisanu ndi chimodzi.

Ali mu sitandade folo, adadwala malungo aubongo, omwe adamupatsa ulumali. Nachisale anasiya sukulu ndipo wakha-la akuvutika kulankhula komanso kuyenda. Amayenda mot-simp'hina kwambiri ndipo samayendanso mtunda wautali.

M'mawa wina, mnyamata wina anamuchita chiwembu Nachisale pamene amkapita ku nyumba ya azakhali ake yomwe inali pa mtunda wa mamita ochepa koma panali nyumba zina pakati pa yakwawoyo ndi ya azakhaliwo.

Mnyamatayo anakokera Nachisale mu khumbi lake ndi kumugwiririra. Munthu wina woyandikana naye nyumba ataona zimenezi anakanena za nkhaniyi kwa mayi a Nachisale. Mnyamatayo anagwidwa mothandizidwa ndi oyandikana nawo nyumba ndipo anamutengera ku polisi ya Ndirande komwe anatsekeredwa kwa masiku angapo asanatulutsidwe pa belo la polisi.

“Tidapita ku One Stop Center yaku chipatala cha QECH komwe zidatsimikizika kuti a Nachisale adagwiridwa komanso kuvulazidwa. Panopa akudwala matenda a kadza mkodzo. Anabowoka pakati pa chiwalo chake cha chikazi ndi kotulukira chimbudzi. Izi zidachitika chifukwa chogwiriridwa. Kuyambira pamenepo wakhala akuchucha mkodzo ndipo nthawi zina amatulutsa chimbudzi paliponse pomwe wakhala,” anadandaula mayi ake.

Mayi ake a Nachisale anali ndi nkhawa kuti mlanduwu sukupita ku bwalo la milandu chifukwa amafunitsitsa kuti chilungamo chichitike.

Iwo anabwera ku maofesi athu ndi kunena zimene zinamuchitikira mwana wawo, “Ndi zowawa kuti ngakhale ndi nakanena nkhanayi ku polisi, woganiziridwayo akadali mfulu ndipo mwana wanga wa mkazi akukumana ndi zowawa”.

Mlanduwu ndinautenga mwachizolowezi. Ndidapita koyamba ku polisi komwe tidatsimikizira kuti mulandu unakanenezedwa ndipo njira zonse zidatsatiridwa. Ndidapitanso ku One Stop Center ya chipatala cha QECH komwe mtsikanayo adathandizidwa ndikutsimikizira mlandu wogwiridwa.

Ndinaona kuti chinachake sichinali m'malo; ofesi ya ozenga mulandu ku polisi inalibe mlandu wa Nachisale. Ndinakayikira chinyengo komabe sindinagonje. Ndinabwerera m'mbuyo, kusunghanitsa zikalata zonse zofunikira kuti amange woganiziridwa mlanduwo ndikutumiza nkhanayi ku ofesi ya oyimira milandu ya boma omwe akutsata mlanduwo ku bwalo la milandu.

Ndimalandira milandu yambiri yotereyi yomwe nthawi zina ndimalephera kuthandiza kuti chilungamo chichitike ku bwalo la milandu, mwina chifukwa chakuti zikalata zinaonongedwa kapena chifukwa chakuti makolo sanachitepo kanthu pa nkhanayo mwana atagwiridwa.

Koma nkhanayi ya Nachisale yatiwonetsa kuti ngakhale njira zolondola zidatsatiridwa, anthu ena osakhulupirika atha kugwiritsabe ntchito njira zosalongosoka kuti chilungamo chisatengeke.

Nkhani ya kamwana

Mayi wina anaganiza zoti apime mwana wake wamng'ono atamumva akulira mwa chilendo kuti, “Amayi ayipweteteka...” Mwanayo anali kulira chifukwa cha ululu wakuvulala ku maliseche ake.

Mwanayo adasowa cha m'ma 10 koloko m'mawa ndipo mayiyo adatumiza mchemwali wake kuti akamuyang'ane mozungulira deralo koma sanamupeze.

Komabe, ali m'nyumbamo, mayiyo adawona Michael Mughogho atanyamula mwana wosowayo ndi juzi yake ili paphewa.

Mwana anali kulira modabwitsa kwinaku akuloza mali-seche ake.

Atamuvula, adawona kuti ku maliseche kwa mwana wake kwatupa komanso kwavulala.

Wozengedwa mlanduyu anali munthu yemwe nthawi zambiri amkakonda kutenga mwanayo kuti azicheza naye ku nyumba kwake ndipo pa tsikuli anabweretsa mwanayo akulira ndi kuloza ku maliseche kwake.

Mayiyo adakafotokozero apolisi za nkhanayi ndipo adatengera mwanayo ku One Stop Center komwe zidatsi-mikizika kuti adagwiriridwa.

Wozengedwa mlanduyo adapezeka wolakwa ndipo adaweruzidwa kuti akhale mu ndende zaka khumi ndi kugwira ntchito ya kalavula gaga pa 11 Marichi chaka cha 2015.

One Stop Center inakhazikitsidwa ndi cholinga chothandiza amayi kapena atsikana omwe agwiriridwa mwachangu ndikuchepetsa kuthekera koti umboni uonongeke monga

momwe zimkakhallira m'mbuyomu. Komabe nkhani zozenga milandu zimavuta chifukwa cha kuchuluka kwa maofesi omwe ogwiriridwa amayenera apiteko makamaka akakhala kuti alibe woyimilira pa mulandu.

Ndimalandiranso milandu yambiri yozunzidwa m'maganizo zomwe zikapanda kusamalidwa bwino zimachititsa kuti atsikana asiye sukulu. Mtsikana amene wazunzidwa m'maganizo amafunikira chilimbikitso kuti apitirize maphunziro. Nkhanza za m'maganizo zimakankhira ana ku banja ndipo zotsatira zake amayamba kugonana adakali a ang'ono zomwe zimawononga thanzi lawo. Ambiri mwa ana okakamizidwa kulowa m'banja adakali aang'ono amakhala ndi moyo womvetsa chisoni, enanso amamwalira msanga.

Udindo wa makolo

Mkulu wina wogwira ntchito ku One Stop Center anati milandu yambiri yogwirira ana ikhoza kupewedwa. Iye wati njira yoyamba yopewera nkhanza zotere ndi kuphunzitsa ana za matupi awo.

“Taona kuti makolo ambiri saona kufunika kouza ana awo za matupi awo. Komabe tsopano ndife okondwa kuti phunziro lotchedwa Life Skills likuphunzitsidwa ku sukulu kuyambira ku pulayimale. Ana amadziwa kuopsa kokhudza mbali zina za thupi lawo,” adatero mkuluyu.

Mkuluyu wati ana akuyenera kuphunzitsidwa mayina a ziwalo zonse zathupi ngakhale zomwe zimawoneka ngati zotukwana komanso mayina omwe ena amagwiritsa ntchito.

Ana ayeneranso kuphunzira kulamulira matupi awo ndi m'mene akumvera. Ayenera kudziwa kuti akagwiritsa ntchi-

to matupi awo molakwika padzakhala zotsatira zoopsa. Izi zikutanthauza kuti ngati wina ayesa kuwazunza kapena kuwagwira molakwika ayenera kuchitapo kanthu.

Pali anthu amene amaphunzitsa ana kufunika kokhala ndi zinsinsi koma mkuluyu akuti ana akuyenera kuphunzitsidwa zinsinsi zoipa ndi zinsinsi zabwino. Ngati zinsinsi zokhudzana ndi nkhani zogonana, ana ayenera kumasuka ndi kunena pamene wina wakhudza kapena kuseweretsa maliseche awo.

“Ana akuyenera kulimbikitsidwa kuti azinena pamene anthu akuwagwira molakwika. Ayenera kuphunzitsidwa kugwira kwa bwino ndi kugwira koyipa. Ngati wina wawagwira molakwika anene ndipo wina akawafunsa kuti asunge chinsinsi atamugwira molakwika anene,” adatero mkuluyo.

Ndalandirapo milandu yomwe ana adaulula kuti munthu wa mkulu adayamba kuwauza kuti asauze aliyense kuti anawapsyopsyona.

Ndinali ndi nkhani ya abambo omwe anali ndi ana a akazi awiri omwe amawapsyopsyona tsiku lililonse akamaliza kudya chakudya cha madzulo pamene akugona. Izi mayi awo sadazitenga ngati za chilendo. Patapita nthawi, bamboyo anayamba kupsyopsyona mwana wawo wa mkazi wa mkulu mobisa komanso mowirikiza.

Iye anamukhazika chete mwanayo pomutsimikizira kuti kukamba nkhani imeneyi kungapangitse mwana wamng'onoyo kuti azichita nsanje.

Posakhalitsa, kupsyopsonako kunafikira kugwira mabere, maliseche ake ndipo bamboyo anamuwuzza mwanayo kuti azimugwiranso. Kwa kanthawi, mtsikanayo anasunga chinsinsi. Nthawi inafika pamene mtsikanayo sanathenso

kusunga chinsinsi.

Koma iye amkaopa kuuza mayi akewo chifukwa anaonera kanema yemwe anaona munthu wina yemwe anali ndi vuto ngati limeneli ndipo analangidwa atauza mayi ake zimene bambo ake amkamuchita. Mtsikana yemwe anali mukane-mayo anamenyedwa mbama ndi kuuzidwa kuti akhale chete.

Posadziwa kuti angawauze bwanji mayi ake, mtsikanayo anafunsa mayi ake ngati angamumenye iyeyo atawauza chin-sinsi ngati mtsikana amene anamuona mu kanemayo. Mayiyo adasokonezeka m'maganizo koma adawamuuza kuti amuy-ankha nthawi ina. Mayiyo anauza mwamuna wake za funso limene mwana wawoyo anafunsa. Mamunayo anadziwa kuti zinthu zimuvuta ngati mkaziyo adziwe chowonadi. Anagan-iza zochitapo kanthu mwachangu kuti izi zisachitike. Iye anafika kwa mtsikanayo ndi kumuuza kuti sadzamugwiranso koma azimupsyompsyona monga mwa nthawi zonse asana-gone ndipo palibe chomwe adzichite mobisa.

Mawu omwe bamboyo adanena adasokonezanso kwam-biri maganizo a mtsikanayo ndipo anapitanso kwa amayi ake kufotokoza nkhani yonse. Mkaziyo adakhumudwa kwambiri koma adadziwa kuti kumufunsa mwamunayo za nkhanayi si-kungakhale kwa bwino ndipo adandifunsa malangizo. Tinali ndi mlangizi wathu amene anayendetsa nkhanayi.

Tinamupatsa uphungu wa momwe angakhalire ndi ma-muna wakeyo ndipo tsiku lina tinamuyitanitsa mamunayo kuti ticheze naye pa msokhano wokamba momwe angalerere ana a akazi m'nthawi ya makono ya chidziwitso chochuluka.

Tinakonza misonkhano ingapo ndi banjali pamodzi ndi mabanja ena kotero kuti panalibe chikayikiro chomwe china-

buka. Banjalo linapulumsidwa ku manyazi komanso kutha kwa banja. Bamboyo anasiya kukhumba mwana wa mkaziyo ndipo atsikanawo akukula kukhala atsikana odalirika. Tidazindikira kuti kukonza njira zopewera ndiye njira yotsimikizika yothanirana ndi nkhanza zakugonana.

Zipembedzo zoyambitsa nkhanza

Catherine ndi msungwana wa folomu 3 yemwe amakhala dera lina mu mzinda Blantyre ndipo ndiwa mpatuko wa chipembedzo chomwe chimalimbikitsa atsikana kuti azikwatiwa msanga. Iye anandipeza kuti ndimuthandize. Catherine ndi mwana wa masiye yemwe agogo ake a akazi pamodzi ndi a malume ake amamukakamiza kuti akwatiwe ndi mwamuna yemwe anamusankhira, mwana wa wansembe wa mpingowo.

“Mpingo wathu umakhulupirira kuti atsikana ayenera kukhala anamwali kuti akhale akazi abwino ndi olemeke-za banja. Ndi mwambo wa mpingowu kukwatitsa ana ali achichepere. Ine ndili ndi maganizo osiyana pa nkhanzi ndi chifukwa chake ndimakana kukwatiwa. Ndinali mu sitandade 7 pamene amandifunsira banja,” adatero mtsikanayo atabwera ku ofesi yanga.

“Ndaona anzanga ambiri (asungwana) akukwatiwa ndi kukhala ndi moyo womvetsa chisoni. Ndikufuna maphunziro ndipo ndidawafotokozera agogo anga za izi. Kuyambira pamenepo amandikwiyira nthawi zonse. Ndinalimba mtima makamaka nditasankhidwa kukaphunzira ku sekondale,” akukumbukira motero Catherine. Mphunzitsi wa mkulu waku sukulu kwake adamulangiza kuti abwere kwa ine kuti ndimuthandize ndipo ndinakauza apolisi kuti achitepo kan-

thu.

“Nthawi ina adandimenya. Anandiotchera zovala zanga zonse ndipo anandikakamizika kuti ndivale mayunifomu akutchalitchi. Ndimkanamizira kuti ndili ndi zibwenzi kuti andisiye. Ndinasintha dzina langa ndikukalemba mayeso a Junior Certificate of Education (JCE) kuti asadziwe ndikalephera chifukwa amanena kuti ndine mwana wopanda nze-ru,” adatero Catherine yemwe mayi ake anamwalira adakali wang’ono. Bambo ake nawonso amkaona kuti mwanayo akuyenera kukwatiwa.

Catherine anafotokoza kuti m’modzi mwa anzake (omwe anakwatiwa msanga) anamwalira akubereka.

“Ndili ndi chitsimikizo chakuti anali wamng’ono kwambiri moti sakanatha kubereka ana. Sindikufuna kukumana ndi zoi-pa zomwe anakumana nazozizi. Ndili ndi khumbo lodzakhala mphunzitsi kapena mtolankhani. Ndili ndi mng’ono wanga yemwe ndikufuna kuti aphunzirensa,” adatero.

Sizinali zophweka kutsimikizira omulera Catherine kuti amulole kupitiriza maphunziro ake. Nkhani yake ndi ya chipembedzo. Otsatira a mpingo akufuna kusunga anthu awo ndipo amakonza maukwati kuti atsimikizire kuti palibe mtsikana amene adzakwatiwe kunjira kwa mpingowo.

Takwanitsa kubweretsa chiyanjano pakati pa Catherine ndi omulera ndipo tikupereka chithandizo kuti chidanicho chisabwerere.

Chochititsa chidwi ndi chakuti Catherine adapeza njira yothawira dongosolo la kumpingo podzionetsa ngati ndi mtsikana woyipa, pokhala ndi abwenzi achimuna pomwe izi sizinali chifukwa chogonana koma kuletsa makolo ndi akulu

kuti asamukwatitse ku banja lililonse.

Anakhoza mayeso ake a JCE koma omulera analimbikira-be kumukakamiza kuti akwatiwe.

“Mpingo wathu umakhulupirira kuti ngati atsikana sakwatiwa msanga, azichita chiwerewere ndi kutenga mimba kunja kwa banja ndipo izi zimabweretsa manyazi m’banja. Akazi ayenera kukhala ku khitchini ndipo asamagwire ntchi-to yakunja, kupatula potumikira zofuna za mamuna wake. Ena mwa amuna otere amamaliza maphunziro awo koma ambiri amangophunzitsidwa ntchito zamanja monga kupala matabwa, kukhoma zidebe koma akulimbikitsidwa kukwati-ra mkati mwa mpingo,” adatero.

Nkhaniyi ndidaitengera ku polisi ndipo gulu linakhazikit-sidwa kuti lipereke uphungu kwa omulera mtsikanayu pakufunika komulola kuti apitilize maphunziro ake popanda zosokoneza. M’banjamo muli mtendere komanso Catherine akupitiriza maphunziro ake ndipo bungwe langa likupereka thandizo la ndalama kwa Catherine. Iye ndi wophunzira wa nzeru ndipo ngati angalimbikire akhoza kukhala chitsanzo kwa anzake omwe ali m’gulu la chipembedzo lomwelo.

MUTU WA CHISANUNDI CHIMODZI

KUPHUZITSA ANA

Akatswiri pa makuludwe a mwana m'malingaliro amati

ena mwa mafunso omwe ana amafunsa amawaphunzitsa kukhala omasuka. Kumasuka kumeneku kumawapangitsa kudalira makolo kapena owalera ndipo izi zimathandiza kuti anawo asapusitsike ndi anthu ofuna kuwagwiririra.

“Ana ayenera kuphunzira nthawi yoyenera kuvomera kapena kukana. Ngati munthu wa mkulu wamuuza kuti achite chinthu chinachake chimene sakufuna, iwo ayenera kukana. Ana ayenera kudziwa kuopsa kwa mchitidwe uliwonse womwe afunsidwa kuti achite,” adatero m'modzi mwa akatswiriwo.

Nthawi zina makolo amalakwitsa popewa kuyankha mafunso a ana. Ngakhale yankho lingakhale lovota koma ndi bwino kuti kholo likhale loona mtima ndi kuyankha m'malo mowasiya ana kuti aphunzire zinthu kuchokera kwa abwenzi kapena kwa anthu achilendo.

Ngati ana akukhulupirira makolo, iwo sapita kwa ena ku-

kapeza mayankho. Ana ayenera kuuzidwa chilichonse chomwe akufuna ku dziwa mwa chilungamo. Izi zikachitika, iwo adzakhala ndi mtima wofunafuna choonadi kwa makolo ndipo sadzapitanso kufunafuna mayankho kwa anzawo.

Akatswiri osiyanasiyana pa nkhani ya makulidwe a mwa-na omwe ndalankhula nawo akuti makolo aphunzire kukhala ndi chidwi ndi masewera omwe ana amasewera. Masewera-wa ayenera kuletsedwa ngati asali abwino kwa iwo.

Ana akuyenera kutetezedwa nthawi zonse popewa zinthu zoopsa zomwe zimachitika moyandikana nawo. Makolo onse akuyenera kuganizira kwambiri za masewera amene ana awo amasewera.

Ana omwe akutha msinkhu amafunikira chisamaliro chapadera chifukwa chakuti pamene matupi awo ayamba kukula, amayamba kukhumbira amuna kapena akazi anzawo. Pa nthawi imeneyi, atsikana amayamba kusamba, amakula mabere pamene ziwalo za anyamata zimayamba kukula ndipo amalota maloto ogonana.

Akuyenera kuphunzitsidwa kuti zizindikiro zonsezi ndi za chibadwa koma sizikutanthauza kuti azigonana. Iyi ndi nthawi yomwe ayenera ku phunzitsidwa za kuipa kogonana adakali a ang'ono, monga mimba, matenda opatsirana pogonana monga HIV ndi Edzi ndi zina monga Chindoko. Akuyenera kulimbikitsidwa kuwonerana makanema abwino osati olaula komanso kuwerenga mabuku abwino omwe amawathandiza kukhala odzidalira. Amakhala ndi chidwi chofuna kudziwa zambiri ndipo kuwapatsa mayankho abwino ku mafunso awo kumawathandiza kuti asapeze zomwe apeza zomwe zingakhale zoopsa.

Miyambo ya makolo monga Chinamwali m'madera aku- midzi kumene ana ambiri m'dziko lathu amakhala iyenera kuloledwa pokhapokha ngati izichitika m'njira yoyenera.

Chikachitika bwino, Chinamwali chimathandiza anawo kukhala ndi makhalidwe abwino. Chinamwali chisaloledwe ngati a chinyamata akulimbikitsidwa kuchita zogonana.

Kale, Chinamwali chimkagwiritsidwa ntchito ngati muyeso ndi makolo wotsimikiza kuti ana akula. Izi sizikufunikanso chifukwa ana ayenera kupitiriza maphunziro awo komanso kuwuzidwa za kuopsa kwa matenda opatsirana pogonana omwe afala kwambiri masiku ano.

Achinyamata akuyenera kuzindikira kuti nkhani zonse zokhudza kugonana ndi zachibadwa ndipo zimabwera pa nthawi yake komanso kuti nkhani zokhudza kugonana sizimafuna kuyesera.

Anawo akuyenera ku phunzitsidwa kuzindikira makhalidwe oipa a ena ndi kupewa kuchita zinthu zowapangitsa kuti ayambe kugonana adakali a ang'ono kapena kuwaika pa chiopsezo chogwiriridwa ndi akuluakulu. Achinyamata akuy-enera ku phunzitsidwanso kukana motsindika.

Atsikana ndi anyamata aphunzire kudziteteza mu njira zosiyanasiyana kuti apewe kugwiriridwa. Nthawi zina sikokwanira kungonena kuti ayi. Kuchitapo kanthu podziteteza pamene akuchitidwa chiwembu ndi kofunikiranso; mwachitsanzo ngati mwamuna wayesera kugwiririra mtsikana, mtsikanayo ayenera kugwiritsa ntchito manja ake moyenera ndi kumenyana wa chiwembuyo. Kumenya kumene kuli kofunikira ndi kopanda chisoni. Kudziteteza ndi chida chabwino cholimbana ndi anthu ochita za chiwembu.

“Makolo ambiri amapewa kuuza kapena kuphunzitsa ana awo zoyenera kuchita ngati wina akufuna kuwagwiririra. Mtsikana akuyenera kuphunzitsidwa pomwe angamenye wogwiririra ndipo mnyamata nayenso azidziwa kuti mkazi wachikulire amene amamunyengerera kuti agone nayenso ndi wogwiririra. Nayenso ayenera kudziwa pomwe angamumenye mkazi ameneyo.

“Takhalapo ndi milandu yomwe anyamata ang’ono-ang’ono amagwiridwa ndi amayi akuluakulu ndikuvulazidwa pa nthawi. Siatsikana okha omwe ali pa chiwopsezo. Anyamata amavulazidwa komanso kutenga matenda kwa amayi omwe ali ndi matenda opatsirana pogonana. Atsikana ndi anyamata onse ali pa chiopsezo,” akuunikira m’modzi mwa ogwira ntchito ku One Stop Center yemwe amathandiza achinyamata tsiku ndi tsiku.

Makolo ayenera kukhala pa tsogolo kuphunzitsa ana awo m’mene angadzitetezere ku chiopsezo cha nkhanza zogonana nthawi zonse. Akatswiri a kakulidwe ka ana amakhulupirira kuti palibe mwana amene ayenera kugwiridwa. Zotsatira za kugwiridwa zimakhala zoipa kwambiri kwa ana. Makolo ayenera kuteteza ana ku mchitidzewu nthawi zonse.

Anthu ambiri amene amachitiridwa nkhanza zokhudza kugonana, anyamata ndi atsikana, akanatha kupeweratu akadadziwa m’mene angazitetezere.

Chimodzi mwa zifukwa zomwe zapangitsa kuti milandu ya nkhanza zokhudza kugonana ichuluke m’dziko muno makamaka kumidzi ndi kubisa milandu yotereyi. Makolo ena amaona kuti ndi zochititsa manyazi kuulula nkhani zogwirira makamaka ngati wachibale wawo wa pa mtima monga amalume kapena mamuna wakhudzidwa.

Taonako akubanja akuchotsa milandu m'mabwalo oweluzwa milandu ponena kuti si bwino kuti m'bale wawo wolakwayo apite ku ndende. Izi zikuchitika m'maboma onse. Mwachitsanzo milandu yokwana 17 yomwe panali umboni womveka bwino idachotsedwa ku bwalo loweluzwa milandu ya magistrate m'boma la Mulanje mu chaka cha 2013.

Ozenga milandu ku polisi analibe mboni ndipo woweluzwa milandu sakanapitiliza ndi milanduyo. Mudzadabwa kumva kuti nthawi zambiri atsikana achichepere amavulazidwa kwambiri ndipo ena sachira koma olakwa amakhala omasuka.

Ndaona kuti milandu yambiri ku Mulanje imakhudza abambo omwe adalangizidwa ndi asing'anga kuti agone ndi ana awo a akazi kuti apeze chuma. Abambo awiriwo adagwirizana zogwirira ana awo. Abambowo anakanenezedwa pomwe ana a akaziwo adauza achibale za zomwe zinachitikazo koma amayi awowo adawateteza amuna awo. Milandu yochitira nkhanza atsikana nthawi zonse imakhala yochuluka koma amayi amasunga chinsinsi.

M'modzi wa anthu ogwira ntchito zoona chisamaliro cha anthu anati kuli mwambo woti amayi amapempha ana awo a akazi kuti asangalatse abambo awo opeza ngati njira imodzi yowaletsa abambo kuti asamachite zibwenzi ndi amayi ena. Mkuluyu anati mwambowu ukukolezera kufala kwa matenda opatsirana pogonana kwa atsikana ku Mulanje. Atsikana samapatsidwa mwayi wokana chifukwa cha maubwenzi amphamvu m'banja.

Zimenezi zikutanthauza kuti makolo sangathe kuphunzitsa ana awo m'mene angadzitetezere. Apa ndipamene timaona kuti aphunzitsi nawonso ali ndi udindo wophunziti-

sa ana momwe angadzitetezere komanso kuthamangira ku polisi akagwiridwa. Nzika iliyonse yosunga malamulo ili ndi udindo woteteza ana athu ku zigawenga. Anthu akuyenera kupanga malo otetezeka kwa ana athu.

Ogwiririra ana ayenera kukumana ndi lamulo mosasamala kanthu za unansi wawo ndi anawo.

MUTU WA CHISANUNDI CHIWIRI

A MPHUNZITSI OGWIRIRIRA ANA

Ndakhala ndikuyendetsa ntchito yothetsa maukwati a ana m'madera awiri a mfumu Kapeni ndi Machin-jiri m'boma la Blantyre ngati gawo la ntchito yanga. Ndinalimbikitsidwa kuti ndiyambe ntchitoyi pambuyo pa kafukufuku wina wosonyeza kuti madera awiriwa ali ndi chiwerengero cha chikulu cha ma ukwati a ana. Zifukwa zazikulu za ma ukwatiwa ndi miyambo ina imene imalimbikitsa ana kuchita zogonana adakali a ang'ono akapita ku Chinamwali (mwambo umene ana omwe atha msinkhu amaphunzitsidwa za kugonana kuti awakonzekeretse kukhala munthu wa mkulu).

Mwambowu ndi wabwino koma umalephera kuthandiza anawo kupewa kugonana adakali a ang'ono. Atsikana nthawi zambiri amagonedwa mokakamizidwa ndipo amakhala ndi pakati ali a chichepere. Amakakamizidwa kukwatiwa ndi amuna akulu kuposa iwo ndi kusiya sukulu.

Pamene ntchitoyi imkapitilira, ndidapeza kuti opalamula milandu yogwiririra ana si anthu wamba okha komanso og-

wira ntchito m'boma. Aphunzitsi amagwa m'gulu ili. Takhalapo ndi milandu ingapo yomwe aphunzitsi apereka mimba kwa atsikana angapo.

Maria

Maria ndi mtsikana wa zaka 15 za kubadwa. Iye amatulutsa misozi mwana wake akulila m'manja pomwe amafotokoza nkhani yake kwa ogwira ntchito ku bungwe la Eye of the Child yemwenso anali ndi misozi.

Mtsikanayu, yemwe ndi wa masiye ndipo anasiya sukulu ali sitandade 7 pa sukulu ya Katete mudara la mfumu Kapeni, anafotokoza zinthu zomwe zidamudabwitsa mkuluyo. Maria ananena kuti maulendo angapo amkatumidwa ndi aphunzitsi ake kuti akasiye mabuku ku nyumba kwawo yomwe ili mtunda wa kilomita imodzi kuchokera ku sukuluyo.

Iye adati poyamba zimawoneka ngati zabwinobwino chifukwa anzake amamuperekeza ndipo amachoka ku nyumba kwa mphunzitsiyu popanda vuto lililonse. Tsiku lina sanaperekezedwe ndi anzake ndipo mphunzitsiyu anamugwira bere lake ndi kuyesa ku mupsopsona koma anakana. Anachenjezedwa kuti asunge chinsinsi, ponena kuti anali mtsikana wabwino kwambiri.

“Ndidauza mkulu wanga yemwe adakwatiwa ndipo amandilera popeza ndine mwana wa masiye koma adangoti ndine wokongola ndipo palibe mwamuna amene sangandifune. Anati poti aphunzitsi anali mbeta, nditenge uwu ngati mwayi. Ndi atsikana angati omwe amapeza mphunzitsi ngati okonedwa wawo? Ndiwe wa mwayi mng'ono wanga,” Maria anafotokoza kwa ogwira ntchito ku bungwe la Eye of the Child.

Maria, yemwe anataya makolo onse aŵiri ali wamng’ono, sanamvetsetse mawu a mchemwali wake. Tsoka ilo adalibe oti amawuzenso. Mawa lake anzake akusukulu adalankhula mogwirizana ndi mchemwali wake uja.

“Ndikumudziwa mphunzitsi ameneyo. Iye ndi munthu wa bwino. Apereka mimba kwa Linley ndipo amasalira mwanayo. Iye ndi wa nzeru. Ndikanakhala iwe sindikanakana,” m’modzi mwa anzakewo anatero.

Iye sanamumvere ndipo anasankha kuti asagwere m’mayesero. Anakana ntchito iliyonse yomwe mphunzitsiyu amamupatsa kunja kwa kalasi ndipo izi zinayambitsa chidani ndi mphunzitsiyu.

“Sindinaganizirepo za khalidwe lake loipali ndipo ndinali wokonzeka kumudzudzula ngakhale kukauza mphunzitsi wa mkulu ngati akanapitiriza kundivutitsa. Mchemwali wanga anapitirizabe kundinyoza komanso kundimana zinthu ngati sopo. Mlamu wanga ndiye yekha amene anali mbali yanga ndipo anandilangiza kuti ndikane aphunzitsiwo. Iye anati sukulu idzakhala ya phindu kwa ine. Koma nthawi zonse mlamu wanga akakamba izi, mchemwali wanga amakukalipira ponena kuti iye akufuna kutikwatira tonse. Mlamu wanga anasankha kusachitapo kanthu.”

Maria adamaliza sitandade 6 ndipo amayembekezera kulowa mukalasi ya Sitandade 7. Komabe mphunzitsiyu adakhalanso mphunzitsi wake. Sukulu yapafupi inali pa mtunda wa makilomita angapo ndipo sakanatha kupita ku sukulu ina. Anasankha kukhalabe pa sukulupo.

“Ndinali ndi mwayi tidalandira mphunzitsi wina wa mkazi pa sukulupo yemwe adayamba kutilangiza momwe tingadzis-

amalire. Ndinali wokondwa kukhala ndi chitsanzo chabwino ndipo ndinali wotsimikiza kudzakhala mphunzitsi,” adatero.

“Komabe, tsiku lina mphunzitsiyo anabwera ku nyumba kwathu. Ndinamupeza akucheza ndi mchemwali wanga. Sanachoke mpaka kunada. Pa nthawi, mlamu wanga kunalibe ndipo anabwera mochedwa kwambiri. Ndinapita kuka-gona ku chipinda kwanga ndipo usiku kwambiri aphunzitsi adalowa ku chipinda kwanga ndi kundigwiririra. Zinali zow-awa kwambiri ndipo ndidadziwa kuti mchewali wanga ada-konza izi. Ndinatenga mimba ndipo ndinasiya sukulu. Sindinathe kukafotokozerwa mphunzitsi wa mkuluyo chifukwa mkulu wanga anandiletsa,” adatero.

Ngakhale mphunzitsiyo amapereka chithandizo pa nthawi ya mimba. Maria anakana kukwatiwa. Amkafuna kupitiriza maphunziro ake koma tsopano zinali zovuta ndi mwan-ayo. Mphunzitsiyo adasamutsidwa kupita ku sukulu ina.

Maria ndi m’modzi mwa atsikana omwe ali ndi ana amene ndawalimbikitsa kuti abwerere ku sukulu. Chinthu choyamba chimene bungwe lathu linachita chinali kuonetsetsa kuti lamulo ligwire ntchito pa mphunzitsi ndinso kuonetsetsa kuti iye atenge udindo wosamala mwanayo.

Nkhani ya chiwiri inali yokhudza kugwiririra komanso kugonana ndi mwana wang’ono. Nkhaniyo inatumizidwa ku bwalo la milandu. Mphunzitsiyo anayimitsidwa pa ntchito pamene akudikira chigamulo chomwe chitha kumutumiza ku ndende. Bungwe la Eye of the Child linatenga ili ngati phunziro pothetsa ma ukwati a ana. Atsikana ambiri amapita ku bungwe la Eye of the Child ndi madandaulo ngati amenewa ndipo abwerera ku sukulu.

Milandu ina simakhudzanso aphunzitsi koma abambo apa banja amene sasamala za tsogolo la mwana wa mkazi.

Bungwe la Eye of the Child lakhazikitsa magulu a amayi, aphunzitsi opuma pa ntchito kapena ogwira ntchito m'bo-ma, magulu a amayi omwe amakhala ngati zitsanzo ndikulangiza atsikana za kuopsa kwa ma ukwati okhudza ana.

“Tikudziwa kuti atsikana ambiri amatha kukana kugonana adakali a ang’ono koma ena amangogwiriridwa ndi abambo kapena achinyamata anzawo. Timawaphunzitsa m’mene angadzitetezere. Timawatengera ku bwalo la milandu omwen-so opereka mimba kwa atsikana. Ena mwa iwo achotsedwa ntchito. Tikuona kuti ntchito imeneyi, yomwe bungwe la Eye of the Child idayambitsa, yapereka mwayi kwa atsikana oti akhale pa sukulu,” anatero Mayi Martha Mbewe, m’modzi mwa atsogoleri a magulu a amayi m’dera la mfumu yaikulu Kapeni mu boma la Blantyre.

Magulu a amayi amagwiranso ntchito ndi anakhungwi a Chinamwali kuti awawunikire mauthenga oyenera kuwauza atsikanawo. Amakhala nawo ku gawo la Chinamwali ndikuwonetsetsa kuti mauthenga otetezeka okha ndi omwe akuperekedwa kwa atsikana.

“Tizindikira kuti chikhalidwe chatu chiyenera kusungidwa koma nkhani zokhudzana ndi kugonana ziyenera kukam-bidwa mosamala. Atsikana ambiri omwe ali ndi ana adag-wa ndi uphungu woyipa womwe adalandira ku Chinamwali. Uthenga uyenera kumveka bwino kuti mchitidwe wogonana sufunika chizolowezi kapena maphunziro,” akutero mayi Mbewe.

Mayi Mbewe adati kusapezeka kwa aphunzitsi achikazi

m'madera ambiri akumidzi ya mafumu Kapeni ndi Machinjiri (mafumu awiri omwe ali malo akuluakulu m'boma la Blantyre) kumapangitsa kuti atsikana azivutika kukhala ndi zitsanzo za bwino. Iye adati magulu a amayiwa akupempha akuluakulu a zamaphunziro kuti atumize aphunzitsi achikazi kumidzi kuti akakhale chitsanzo za bwino kwa atsikana.

“Nthawi zambiri timaitana anamwino ndi akatswiri ena achikazi kuti akalankhule ndi ana a sukulu m'derali kuti atsikana aphunzire kukhala ndi maloto a akulu. Makolo amaitanidwa ku masiku omwe akastwiriwa amalankhula ndipo izi zimathandiza kusintha maganizo,” anawonjezera motero.

Bungwe la Eye of the Child silikuchepetsa ma ukwati a ana okha komanso likudziwitsa anthu za nkhanza zogonana. Imaphunzitsanso makolo njira zosiyanasiyana zothandizira ana awo kuti athe kuzindikira chiopsezo chogwiriridwa ndi kudziteteza.

“Ana ayenera ku phunzitsidwa kuzindikira nkhanza komanso kapewedwe kake ndipo ngati ndikotheka, m'mene angazitetezere. Kugwiriridwa kumakhudza kwambiri miyoyo yawo ndipo sikuyenera kuloledwa kuchitika n'komwe,” adawonjezera.

Malinga ndi kafukufuku yemwe anachitika ku madera a mafumu Machinjiri ndi Kapeni, nkhani zogwiririra ndi maukwati a ana a ang'ono zimabwera chifukwa chosowa chitetezo ndi chisamaliro cha makolo makamaka m'mabanja amene akutha.

Pali mabanja ambiri omwe mutu wa banja ndi amayi kape-na mwana. Makhaliidwe m'mabanja ambiri okhala ndi kholo la mayi okha amayika ana pa chiopsezo chogwiriridwa m'nji-

ra ziwiri za zikulu.

Ena mwa amayiwa amafula mowa womwe amuna amabwera kudzamwa ndipo ena mwa amunawa amakopa atsikana kuti agone nawo. Nthawi zina amayi omwe amuna awo anamwalira amakwatiwanso ndipo abambowa amakakamiza at-sikana kuti agone nawo.

“Azimayi ena ofooka amasiya amuna awo kuti apitirize mchitidwe wotere koma ntchito yathu ndikuwawonetsa kuti atsikana sayenera kuchitiridwa nkhanza. Tikuwalimbikitsa atsikanawo kuti aziulula ngati akuluakulu awakakamiza kugona nawo kapena kuwapatsa mphatso popanda zifukwa zomveka. Ntchitoyi ikuthandiza ndipo nthawi zambiri talepheretsa mchitidwe wogwiririra,” akutero mayi Mbewe.

Iwo anafotokozanso kuti mabanja omwe ana amasungana okhaokha amayenera kulandira thandizo ngati njira yotezera ana ku nkhanza zogwiriridwa. Ambiri mwa ana otere nthawi zambiri amafunikira thandizo pa zaulimi monga kupereka feteleza. Ngati apeza izi ndi zofunika zina, atsikanawa sangazunzidwe.

“Timaonetsetsa kuti mafumu akuyika anawa pa kaundula wa omwe apeze zipangizo zotchipa mu ndondomeko ya thandizo la zipangizo za ulimi. Ana amenewa kawirikawiri, chimene amafunikira ndi chitsogozo cha momwe angadzisamalire ndi kudziteza ku nkhanza zogwiriridwa. Timawalimbikitsa kukhala otsimikiza ndi kuganizira za tsogolo lawo. Tikuwona kuti zomwe amafunikira ndi chilimbikitso chochulukirapo ndipo ambiri a iwo safunikira kukhala kumalo osungira ana amasiye, komwe amakumananso ndi nkhanza,” akutero a Mbewe.

Mabanja omwe ana amasamalana okhaokha amafunikira chithandizo chochuluka. Anawo ali pa chiwopsezo chifukwa amatha kukakamizidwa kulandira thandizo lochepa kuchokera kwa abambo omwe pamapeto pake amawachitira nkhanza, makamaka atsikana.

“Timalimbikira kufikira atsikana omwe ali munyengo yoteroyo kuti asalowe m’mayesero,” akutero mayi Mbewe.

Maria akuti anakhululukira mchemwali wake koman-so mphunzitsiyo koma analumbira kuti sadzaiwala zomwe anakumana nazo. Amalankhula ndi atsikana ambiri pa misonkhano yosiyanasiyana yomwe imakonzedwa ndi magulu a amayi, kulimbikitsa atsikana kuti azimenyera ufulu wawo, kukhala pa sukulu, kupewa ku kwatiwa ali achichepere komanso kudziteteza ku nkhanza zogonana.

“Ndinakakamizika kupirira kuzunzika kumeneku koma sindikufuna kuti atsikana ena akumane ndi zimene ndinakumana nazo pokhala mayi ndili mwana. Chikanakhala chisankho changa, ndikanamva mosiyana. Koma uku kunali kugwiriridwa ndipo ndikufuna kuti atsikana kapena achinya-mata azitetezedwa ku izi,” akutero.

Maria tsopano ali mu sitandade 6 ndipo sanataye mtima wofuna kukhala mphunzitsi kapena namwino. Iye akuwona kuti kubwera kwa ntchito yoyendetsedwa ndi bungwe la Eye of the Child ndi yotumidwa ndi Mulungu ndipo ikuyenera kufikira madera ambiri a dziko lino. Ntchitoyi yapereka moyo wa tsopano kwa atsikana ndipo yawapatsa chidziwitso.

“Sindipumula mpaka nditakwaniritsa cholinga chan-ga. Munthu amene anandigwiririra uja analandira chilango choyenera. Ndikuganiza kuti ili ndi phunziro la bwino kwa

akuluakulu onse omwe sangathe kulemekeza ufulu wa ana omwe ali pansu pa ulamuliro wawo. Aphunzitsi omwe ali ndi zizolowezi ngati izi tsopano ayenera kusintha kapena kuchotsedwa ntchito monga momwe zinakhalira ndi aphunzitsi anga. Sindingamvere chisoni aphunzitsi ngati awa chifukwa cha ululu umene ana amene amawagwirira amakumana nawo,” akutero Maria.

MUTU WA CHISANUNDI CHITATU

ANA ACHILEMA

Dorothy ndi mtsikana wa zaka 16 za kubadwa yemwe amakhala ku Chilaweni mudera la mfumu yaikulu Machinjiri mu boma la Blantyre. Iye ndiwa khungu ndipo wakhala ndi agogo ake kwa moyo wake wonse. Makolo ake anamwalira ali wamng’ono kwambiri. Agogowo ndi wokalamba kwambiri ndipo zimawavuta kusamalira Dorothy.

“Ndinasiya kuona ndili mu sitandade folo. Mutu unandipweteka kwambiri. Agogo anga sananditengere ku chipatala koma m’malo mwake ndinapatsidwa mankhwala azitsamba omwe anandipaka m’maso. Ndinasiya sukulu ndipo mwamuna atabwera kudzapempha kuti andikwatire, agogo anga anavomera,” iye anatero kwa wogwira ntchito ku bungwe la Eye of the Child.

Mamunayo ndi msodzi ndipo anamusiya Dorothy kupita ku nyanja ndipo sanabwerenso.

“Nditapita padera, ndinabwerera kukakhala ndi agogo anga koma sindingathe kupita kumunda kapena kuchita

chilichonse chopindulitsa. Agogo anga ndi okalamba kwam-biri sangapitenso ku munda. Timadalira anthu a chifundo amene amatipatsa chakudya. Nyumba yomwe tikukhalayi inamangidwa ndi mamuna wanga. Ndinavomera kukwatiwa chifukwa ndi mkafuna munthu woti atithandize. Kwenikwe-ni mamuna wanga adaganiza zondikwatira atandipatsa pa thupi. Sizinali chifukwa cha chikondi. Anatengerapo mwayi pa vuto langa,” akutero Dorothy.

Mamunayu, yemwe anali wa mkulu kwa iye ndi zaka zam-biri, ndi wachibale chapatali ndi gogoyo. Agogo aja adalimbikitsa banjalo ndi chiyembekezo choti Dorothy asamalika.

“Ndikhoza kufotokoza kuti kugonana kwathu koyamba kunali kugwiridwa ndithu. Sindinakonzekere kugoned-wa. Ndinavutika kwambiri koma ndinauzidwa kuti iyi nde banja. Komabe bamboyo anathawa pamene ndimamufuna. Ndikanakonda ndikadakhala kuti ndinamuona munthu yemwe anandigwiririrayo. Ndikanakana ndi kusankha kupitiriza maphunziro anga. Agogo anga amandiuza kuti ali ndi zaka zopitirira makumi asanu ndi awiri ndipo ndikudziwa kuti nditsala ndekha akadzamwalira. Sindikuganiza kuti mamuna wanga amandifunanso. Ndikuchita mantha,” adafotokozera ogwira ntchito ku bungwe la Eye of the Child.

Chinthu choyamba chimene bungwe la Eye of the Child lidachita chinali kupeza ndalama kuchokera kwa anthu akufuna kwa bwino kuti amange nyumba ya bwino ya banjalo. Banjalo linalibe ziwiya zophikira za bwino, zofunda kape-na chakudya zomwe zimayenera kuperekedwa. Bungweli lidayenera kupeza chakudya chokwanira banjali kuonjezelapo kuyesa kupeza abale omwe angawathandize kusamalira gogoyo ngati zolinga zotengera Dorothy ku sukulu ya akhungu

ya Mulanje zitatheka.

Kodi Dorothy adzachita chiyani akaphunzira ku sukulu ya akhungu? Adzaphunzira luso lomwe lingamuthandize kupe-za ndalama komanso kupeza zofunika pa moyo wake.

“Ndamvapo nkhani za anthu akhungu amene zinthu zikuwayendera bwino; momwe aphunzirira maluso atsopano omwe amawathandiza kudzidalira okha osati kudalira kupempha. Inenso ndikufuna kukhala wosiyana. Sindikufuna kupempha. Ndikufuna ndizitha kukonza chakudya, kuchapa zovala zanga ndi kuchita zinthu za mtundu uliwonse ndekha. Ndikufunanso kuphunzira zinthu zina monga kusoka ndi kupanga zovala zomwe ndingathe kugulitsa. Pempho langa ndilakuti akufuna kwa bwino anditumize ku sukulu. Ndamva kuti anthu ngati ine amatha kulima, kuweta nkhu ku koman-so kupanga ndalama,” akutero Dorothy wotsimikiza mtima.

Agogowo adati akukhulupirira kuti Dorothy akhoza kuchita bwino chifukwa ali ndi mtima wolimbikira.

“Ndimazona kuti ndine gwero la mavuto ake. Ndikukhulupirira kuti ndikanamutengera ku chipatala pamene adadwala, sakanakhala wa khungu. Zinali zotsatira za umbuli wanga. Ndinalakwitsanso chimodzimodzi pamene ndinamulimbikitsa kukwatiwa. Ndimatenga udindo pa mavuto a mwana wanga,” akutero agogowo uku akugwetsa misozi.

Chodabwitsa ndi chakuti Dorothy ndi yemwe amatontho-za agogo ake ndi mawu a chifundo.

“Chilichonse chimene agogo anga anachita chinali chifukwa cha chikondi. Mwana wawo wa mkazi anamwalira ku chipatala nthawi imene anadwala, mwina amkaopa kuti inenso ndikafera ku chipatala. Kodi tingawaimbe mlandu chifukwa

cha zimenezi?” Dorothy anafunsa.

Dorothy akuti agogo ake anali ndi zolinga za bwino; kuphatikizapo kumukakamiza kulowa m’banja.

Agogo aja amkafuna kuti munthu adzisamalira Dorothy wakhungu osadziwa kuti iyeyo ndi mfiti chabe yomwe cholinga chake chinali kungokwaniritsa chilakolako chake basi.

“Choopsa chenicheni chimene ndimachiona pa moyo wanga ndi chogwiriridwa. Sindingathe kudziteteza ngati mwamuna ali ndi zolinga zoipa. Nthawi zambiri ndimamva ndemanga zomwe abambo amanena zokhudza thupi langa ndipo ndimachita mantha. Ndimamva abambo akulankhula mawu otere. Ndikanakonda ndikanatha kuwaona, ndikukhu-lupirira kuti nditha kukhala mkazi wabwino. Ena amafika mpaka ponena kuti ndinakwatiwa kalekale. Ndikuwopa kuti amuna ena atha kupezerapo mwayi pa vuto langa ndikundig-wiririra. Kugonana koyamba kunali kowopsa ngakhale ndi-nauzidwa kuti chinali chiyambi cha banja. Ndimadzimva kuti ndinagwiriridwa ndipo nthawi zonse ndimakhala ndi mantha kuti ndidzakumananso ndi zimenezi,” akufotokoza motero Dorothy.

Bungwe la Eye of the Child likufuna Dorothy atapita ku sukulu ya akhungu ku Mulanje. Iye akuti ichi nde chokhumba chake chokhacho.

MUTU WA CHISANUNDI CHINAYI

CHITHANDIZO

Nkhanza zochitika pogonana zingapewedwe ngati

aphunzitsi ndi makolo onse achita khama pothetsa mchitidwewu. Makolo ayenera kudziwa ziopsezo za nkhanza zogonana, m'mene zimachitikira, komanso m'mene njira zothandizira ozunzidwawo zikhoza kukhazikitsidwira.

M'modzi wa ogwira ntchito ku One Stop Center ku chipatala cha QECH akuti pali makhalidwe omwe ana amagawa-na monga gawo lakukula kwawo. Iye wati makolo akuyenera kutsatira mwa chidwi kakulidwe ka ana awo. Izi zimawathan-diza kuti azindikire kusintha komwe kumachitika chifukwa chogwiriridwa. Ndakhala ndikukamba za njira zodzitezera m'mitu yapitayi koma tsopano tikuyenera kuyang'ana zomwe zimachitika mwana akagwiriridwa.

Zizindikiro za mwana yemwe wagwiriridwa zimatha kukhala za ku thupi ngati kuvulala ku maliseche. Mwana akhoza kukhala ndi vuto pokodza. Kulephera kuyenda bwinobwino kapena kusonyeza zizindikiro za ululu polankhula zithanso kukhala zizindikiro zogwiriridwa ndipo muyikepo

chidwi mukaona izi.

Zindikiro zowonekeratuzi siziyenera kunyalanyazidwa. Chifukwa choopa kukwiyitsa makolo, ana ambiri samasuka kunena zambiri za kugwiridwa. Ndi udindo wa makolo kuthamangira ndi anawa ku chipatala kuti akalandire chithandizo mwansanga, umboni monga umuna usanachotsedwe.

Akatswiri amati zizindikiro zina za m'malingaliro zimakhala zovuta kuzizindikira mwa ana. Izi zikuphatikizapo kutayika kwa dzidzidzi kwa chidwi pa maphunziro, kusokoneze-ka kwa tulo, mantha, kutopa, kusowa kwa njala, nkhanza, kunama, ndi kukopa amuna, mwa zina, zitha kukhala zizindikiro za zotsatira za nkhanza zogonana ndipo ziyenera kufufuzidwa.

Zizindikiro za m'malingalirozi ndi zovuta kwa makolo ambiri koma kholo likhale ndi chidwi nthawi zonse poonesetsa kusintha kwa dzidzidzi kwa ana awo. Ngati mwana nthawi zonse amakhala wokondwa ndipo mwadzidzidzi aku-makhala chete ndi wosakodwa, nthawi zambiri izi zimakhala zizindikiro zakuti chinachake chalakwika. Izi ziyenera kukha-la chifukwa chodera nkhwawa.

Ndi bwino kuti mwana akagwiridwa, makolo asamale posaoneka ngati akuimba mlandu wogwiridwayo kapena kumuweruza. Imeneyi imakhala nkhani yokhudza maganizo ndipo ngati makolo sayitenga mosamala, ingapweteke mwana amene wangokhala mkhole ndipo sakuyenera kuimbidwa mlandu chifukwa cha kugwiridwako.

Izi zikachitika, makolo akuyenera kukapeza thandizo la akatswiri monga kupita ku One Stop Center kapena chipatala chili chonse komanso ku polisi. Iwo sayenera kuyesa

kuthetsa vutolo pa okha chifukwa chakuti iwo alibe ukadau-lo wothana ndi vutoli pa okha ndipo atha kuononga zinthu.

Makolo akulangizidwa kuti azilimbikitsa mwanayo kuti alankhule ndikupereka zambiri zomwe zingathandize akafika ku chipatala.

Nthaŵi zina makolo amathamangira ku chitapo kanthu pa okha. Izi sizoyenera chifukwa zimabweretsa mavuto ambiri chifukwa zimalephera kuthetsa vutoli.

Ndinalandira mulandu wogwiririra kuchokera kwa kholo lomwe linali linatengera kale lamulo m’manja mwake ndipo mulanduwo sunayende bwino ku bwalo loweluza milandu.

Mtsikana wina adagwiridwa ndi bambo wina m’mbali mwa mtsinje. Anthu omwe amachapa m’mbali mwa mtsinje-ataona izi adathamanga ndikumugwira bambo wa chiwembuyo. Pamene anthu adali pa ulendo wotengera bamboyo ku polisi, bambo ake a mtsikanayo adatulukira ndi kumemenya m’mutu bambo wa chiwembuyo amene adakomoka kwa masiku atatatu. Pa chifukwachi, bambo ake a mwana adamangidwa pa mlandu womenya ndi kuvulaza munthu.

Titha kukhala ndi maganizo osiyana koma bwalo la milandu likanatha kuzenga bambo wa mwanayo mulandu wakupha ngati wogwiririrayo akadawalira. Tikukulangizani makolo nonse kuti mukhale odekha ndi kulola kuti lamulo ligwire ntchito moyenerera.

Kugwiririra ndi mlandu wa ukulu ndipo makolo atha kut-simikiziridwa kuti lamulo limagwira ntchito pa oganiziridwawo ndipo iwo asatenge lamulo m’manja mwawo, zomwe pamapeto pake zimasokoneza miyoyo yawo.

Mlandu wogwiririra umakhala wovuta kwambiri ngati m'modzi wa makolo kapena wa chibale wapa mtima akukhudzidwa.

Ndikukumbukira mu umodzi mwa mtsutso womwe udakonzedwa ndi bungwe la Eye of the Child, panali maganizo osiyasiyana koma mbali ili yonse inali ndi mfundo zothandiza ngati zinthu zitayendetsedwa bwino.

Ena anali ndi maganizo okuti ngati kholo lagwiririra mwana, banja lithetsedwe ngati njira yoonetsa kuti khololo latalikira mwanayo. Maganizowa anatinso kholo logwiririralo lizikatsekeredwa ku ndende ndi cholinga choti litalikire mwanayo ndipo mwanayo adzakula ndi kuiwala chowawa-cho. Zinadziwika kuti kusiya kholo logwiririrako sikungath-andizire kukula bwino kwa mwanayo. Mwanayo ayenera ku-tetezedwa mu njira iliyonse.

Kholo limene lagwiririra mwana ndi chilombo chimene sichiyenera kuloledwa kukhala pafupi ndi mwanayo. Ngati umboniwo suliwokwanira kuti munthu aimbidwe mlandu ndiye kuti chisudzulo chikhale njira yothetsera vutolo apo ayi, kholo lolakwa lisasiyidwe kumangoyendayenda m'misewu kuopa kuti angadzachitenso chimodzimodzi kwa ana ena. Mfundo imeneyi ikutsindika pa umboni wakuti anthu ena ogwiririra anawo amagwiririranso ana a ena.

Anthu oterowo, mtsutsowo unati, ndi oopsa kwa anthu ndipo sayenera kusiyidwa afulu.

“Tili ndi abambo ambiri amene akuyenera kukhala m'ndende tsopano koma amayi ena anasankha kunyalanyaza ululu wa uchembere ndi kulola chilombo cha munthu kuchitira chipongwe mphatso ya mtengo wapatali imene Mulungu

anawapatsa. Amayiwa amafunikira thandizo lathu. Tiyenera kufalitsa uthenga uwu ku dziko lonse: Munthu amene wagwiririra mwana wanu wa mkazi ndi chilombo ndipo ayenera kupita kumene iye akuyenera- ku ndende,” anatero m’modzi mwa anthu amene anali pa mtsutsowo, ndipo anthuwo anawomba m’manja kwambiri.

Komabe, ena anali ndi maganizo akuti kusudzulana kape- na kutsekeredwa mu ndende sinjira yothetsera vutolo. Iwo amaona kuti olakwa amafuna thandizo la uzimu kapena up- hungu wamba. Kuwatsala ngati akhate sikungathetse vutoli, izi zikhoza kuyambitsa vuto lina la kutha kwa mabanja. Iwo anati ambiri mwa anthu amene amachita zimenezi ndi anthu omwe ali ndi kuthekera kosamalira banja lawo.

“Mabanja ena ali ndi ana ambiri. Wosamalira banja akatse- keredwa m’ndende, ana ena onse amasanduka osowa, ndiye tikhala tapindula chiyani?” adafunsa m’modzi pa mtsutsowo.

Gululi lidawona kuti upangiri woyenera komanso kuku- mana kwa uzimu kungathetse zomwe zakhazikika ndiku- manga ma banja. Mtsutso pa nkhanayi ukupitirirabe koma ambiri akuti kholo lomwe lagwiririra liyenera kukumana ndi lamulo.

Kuli konse komwe mtsutsowu ungatitengere, nkhawa ya a za umoyo ndi a boma ndi mpumulo womwe mwana amawu-funa ngati wagwiriridwa.

“Tikufuna kuti makolo apeze chithandizo chamankhwa-la komanso malamulo ingakhale iwo asakufuna. Khanza ya mtundu uli wonse kwa mwana siyololedwa. Aliyense amene wazunzidwa ayenera kuthandizidwa. Changu chimathandiza kuti thandizo loyenera liperekedwe. Mlandu wogwiririra uk-

hoza kusokoneza tsogolo la maphunziro komanso maunansi a mwanayo,” anatero katswiri wina ku One Stop Centre.

Mkuluyu akuti makolo asatangananidwe ndi kufuna kubwenzera kwa yemwe wagwiririra mwanayo. Kholo liyenera kuganiza zomuthandiza kaye mwanayo. Ana ena amagwiriridwa kangapo mwina chifukwa choopsezidwa kapena wogwiriridwayo ndi munthu amene amamulemekeza ndipo safuna kumukhumudwitsa.

Ana ena amanamizira kusangalala ndi nkhanzazo kuti akondweretse wowachitira nkhanzayo ndipo makhalidwe oteroyo amachititsa kuti makolo asadziwe zomwe zikuchitika kufikira zinthu zitayipa.

Mwana amene wachitiridwa nkhanza amaonetsa zizindikiro monga tafotokozera pa mwambapa ndipo makolo ayenera kusamala ndi zizindikiro zimenezo. Kufikira anawo kuyenera kukhala kwa nzeru apo ayi chowonadi sichidzadzizika ndipo anawo adzapwetekedwa.

Katswiri wina wa za malingaliro a ana anati: “Ngati ogwiriridwayo sanasamalidwe bwino amasanduka chigawenga ndipo zidzawonongetsa anthu ndalama zambiri m’tsogolo. Iye adzaona dziko lapansi ngati malo omwe kuvulaza munthu ndi chinthu chapamwamba kwambiri.

“Kuzindikira msanga ndi kupereka chithandizo kungathandize kukonzanso anthu otere, omwe pamapeto pake amakhala nzika zabwino za dziko.”

MUTU WA CHIKHUMI

ZIZINDIKILO

Nkhanza zogwiririra zimaika ana pa chiopsezo chachikulu monga cha matenda ndi kuvulazidwa kwe-nikweni. Nthawi zina atsikana omwe amachitiridwa nkhanza zotere amatha kutenga mimba ndi kukakamizidwa kukwatiwa adakali a ang’ono zomwe zimawachotsera mwayi wophunzira.

Akuluakulu a za umoyo akuti milandu yogwiririra ikupitilira kuchuluka. Zifukwa za kuchulukaku zitha kukhala kusokonekera kwa makhalidwe a anthu ambiri. Koma anthu ena amati ichi ndi chizindikilo cha kukula kwa chidziwitso komwe kwalimbikitsa anthu kuti aziulula nkhaniyi.

Ndikukhulupirira kuti anthu akhala akuzunza ana awo nthawi zonse koma nkhani zotere sizimaulutsidwa ndi ofalitsa nkhani chifukwa anthu adasankha kukhala chete. Anthu aphunzitsidwano ndi kuzindikira kufunika koteteza ufulu wa ana.

Ndachitapo kanthu pakulimbikitsa boma kuti likhazikitse malamulo monga Child Care, Protection and Justice Act

(2010) omwe amafotokoza za ufulu ndi ntchito za osamala ana ndi makolo. Makolo ndi osamalira ana komanso oweruza za tsopano akuchita chidwi pa chisamaliro cha mwana.

Ntchito ngati ya bungwe la Eye of the Child yomwe idakhazikitsidwa moyeselera pofuna kudziwitsa anthu za lamulo la tsopanolu mu boma la Blantyre m'madera a mafumu Machinjiri ndi Kapeni omwe ali ndi anthu ambiri ikuthandiza podziwitsa anthu za kuopsa kwa kugwiriridwa komwe kumabweretsa kuvulala kapena kutenga pakati.

Kugwiririra kumakhala ndi zotsatira zambiri, kotero ngati tikufuna kuthetsa ma ukwati a ana, aliyense ayenera kudziwa kuti kugonana kuyenera kuchitika m'banja mokha.

Ndikuzindikira kuti kudziwitsa anthu za kuopsa kwa kugwiriridwa kapena ukwati wa ana, kusiya sukulu, kugwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo, imfa za uchembere, matenda opatsirana pogonana ndi matenda ena monga kadza mkodzo kungathandize kwambiri.

Okhudzidwa monga mafumu, azipembedzo, nthumwi za boma monga owona za malamulo, a zaumoyo wa anthu ndi mabungwe a za umoyo akuyenera ku chitapo kanthu pofuna kuthetsa ma ukwati a ana.

Bungweli lachita mgwirizano ndi atolankhani pofuna kuwonetsetsa kuti ufulu wa ana ukudziwika kwa anthu. Posachedwapa, bungweli lidakonza gawo lophunzitsa atolankhani ndipo izi zipitilira. Zinadziwika kuti atolankhani amatenga gawo lalikulu pa kudziwitsa anthu nkhanu ngati izi.

Ndikudziwa kuti atsikana ayenera kupatsidwa mphamvu zolimbana ndi makolo kapena akulu omwe amawakakamiza kulowa m'banja adakali a ang'ono ndipo m'malo mwake

apitirize sukulu. Kugwiridwa kumabweretsa mimba adakali a ang'ono ndi ma ukwati a ana zomwe zimapangitsa kuti pakhale umphawi wa dzaoneni.

Ndimadalira ogwira ntchito zosamalira ana, atsogoleri a m'mudzi ndi mabugwe azamalamulo, atsogoleri a m'mudzi ndi ogwira ntchito olimbikitsa chilungamo motsogozedwa ndi lalamulo la Child Care, Protection and Justice Act (2010). Makolo amaletsedwa kukwatitsa ana awo koma izi zikuyenera kufalikira ku magulu achipembedzo, kutisakuyenera kumangitsa ma ukwati a ana.

Mfumu Kapeni, yomwe yayamikira ntchito yabwino yom-we bungwe la Eye of the Child likuchita m'dera lake, yati nkhanza zogonana ndi ma ukwati a ana zimagwirizana. Iye wati atsikana ambiri amagonana mokakamizidwa ndi anzawo kapena anthu akuluakulu omwenso amawakakamiza kuchita zinthu zoipa.

“Uthenga kwa anthu onse ndi wakuti atsikana kapena ana asonetsedwe mchitidwe wogonana. Atsikana ayenera kulo-ledwa kumaliza sukulu ndi kukwatiwa ali ndi zaka zoyenera. Pali makolo ena amene amavulaza ana awo koma sadziwi-ka. Yakwana nthawi yoti asiye nkhanza zonsezi. Atsikana amakhala pa chiwopsezo ngati agonana adakali achichepere,” adatero.

Ntchito zomwe bungwe la Eye of the Child likuchita ndi monga kuyendera sukulu, kupanga magulu a amayi ndi misonkhano ya makolo, kuphatikizapo aphunzitsi ndi anthu pozindikira kuopsa kwa nkhanza zogonana ndi ma ukwati a ana.

Bungweli likakumana ndi mtsikana yemwe akukhala ndi

bambo wa mkulu, limakokera bamboyo ku polisi chifukwa malamulo amamveka bwino; mwana wosafika zaka 16 sayenera kukwatiwa. Mwamunayo ali ndi mlandu wogwiririra komanso kuba anthu ndipo akuyenera aweluzidwa ndi lamulo.

Mphunzitsi wa pa sukulu ya Nasengwe pafupi ndi malo ochitira malonda a Lunzu m’dera la mfumu yaikulu Kapeni wati chikhazikitsireni ndondomekoyi, waona kusintha kwa kasamalidwe ka atsikana pa sukuluyo.

“Atsikana athu ambiri nthawi zambiri samkapita ku sukulu. Tinaona kuti zimenezi zinachitika chifukwa cha kugonana ndi amuna akuluakulu. Akuluakulu ambiri tsopano akuopa kuimbidwa mlandu ndipo atsikanawo akusiyidwa okha. Tikuona manthawa ndi omwe abweretsa kusinthaku. Ntchitoyi ipitirire. Atsikana ambiri amakakamizika kuchita zogonana kuti apeze ndalama pamene ena amachita mokopeka ndi makolo awo. Tsopano zikuwoneka kuti ali yense akudziwa kuti kukakamiza atsikana kugonana ndi mlandu,” akutero.

MUTU WAKHUMINDI CHIMODZI

CHILANGO

Ndikufuna kuyamika mabwalo a milandu omwe ama-pereka zilango zokhwima. Chilango chachikulu pa mulandu wogwiririra ndi kukhala ku ndende kwa moyo wonse koma nthawi zina mabwalo oweluzwa milandu ali ndimphamvu zopereka chilango chochepera monga zaka khumi munthu ali ku ndende akugwira ntchito ya kalavula gaga zomwe zimadzetsa nkhawa pakati pa omenyera ufulu wa ana ndi ma bungwe ena.

Mulandu umodzi wodziwika ndi wa Canaan Kaunda wa zaka 25 zakubadwa yemwe adalamulidwa kukakhala ku ndende kwa zaka 14 akugwira ntchito ya kalavula gaga chifukwa chogwiririra mwana wa zaka zisanu za kubada ku Lupaso ku Mzuzu pa tsiku la Khristimasi chaka cha 2014.

Patangotha masiku asanu chigamulochi chitaperekedwa, bwalo lomweli ku Mzuzu, lidalamulanso Richard Chisale wa zaka 33 zakubadwa kuti akhale ku ndende kwa zaka 14 ndi kugwira ntchito ya kalavula gaga chifukwa chogwiririra mtsikana wina wa zaka zisanu zakubadwa komanso zaka

zitatatu chifukwa chogwira malo osayenera mwana wa zaka zisanu ndi ziwiri ku Luwinga Area 1B pa 9 Janyuwale chaka cha 2015.

Anthu onsewa anavomera kuti ndi olakwa ndipo analandira chigamulo. Iwo adapempha bwalo loweluzza mulandu kuti liwapatse chilango chochepa ponena kuti ndi osamalira ma banja awo.

Komabe, woimira boma pa milandu, Lone Tembo, adapempha kuti anthuwa alandire chilango chokhwima kuti ena atengerepo phunziro.

Yemwe anaweluzza milandu yonseyi, Anthony Banda, adati amuna ngati amenewa sakuyenera kukhala pagulu chifukwa amabweretsa mavuto kwa atsikana omwe amawakakamira m'maganizo kwa nthawi yayitali. Chifukwa chake, adawala-mula kuti akakhale ku ndende kwa zaka 14 akugwira ntchito ya kalavula gaga aliyense.

Pothira ndemanga pa zigamulozi, wachiwiri kwa wofalitsa nkhani za apolisi mu mzinda wa Mzuzu adati zigamulo zokhwima ngati izi zathandiza kuchepetsa milandu yoyipa ndi 25 pa 100 iliyonse, mu mzinda wa Mzuzu.

“Mu chaka cha 2013, tidali ndi milandu 53 yogwiririra ana pomwe mu 2014 tidali ndi milandu 40. Izi zikuyimira kuchepa kwa pafupifupi 25 pa 100 aliwonse mu mzinda wa Mzuzu.”

“Tikuona kuti kuchepaku kudachitika makamaka pa zifukwa ziwiri; choyamba, misonkhano yolumikizana ndi nthambi ya chitetezo cha m'madera yakhala ikuchita m'madera ndi atsogoleri osiyanasiyana okhudza chitetezo cha ana. Kachiwiri, tikukhulupirira kuti zigamulo zokhwima bwino

zomwe mabwalo oweluzza mulandu athu akhala akupereka kwa olakwa zathandizanso. Ndipo tikuwayamikira chifukwa cha zimenezi,” adatero a Saulosi.

Iwo adapempha anthu amumzindawu kuti awonesetse ndi kukanena ku polisi nkhanza zili zonse zochitikira ana.

“Amene amachita nkhanzazi nthawi zambiri ndi abambo owapeza, amalume, okhala nyumba yoyandikana, ndipo nthawi zina ndi amuna ogwira ntchito za pakhomo,” adatero Sergeant Saulosi.

Ngakhale zilango zokhwima zikuperekedwa kwa anthu opezeka olakwa m'boma la Nkhata Bay, khalidwe lonyansali likuoneka kuti likukulirakulira pamene bambo wina wa zaka 42 ali m'manja mwa apolisi chifukwa chogwiririra mwana wake wa mkazi wa zaka zinayi.

Boma la Nkhata Bay lakhala ndi chiwerengero chokwera cha milandu yogwiririra ana. Oweluzza milandu mu bomali, Billy Ngosi, adanena posachedwapa kuti milandu yoposera 24 yogwiririra ana yafika kubwalo la milandu chaka chino chokha.

Posachedwa, Blackson Mhone yemwe amachokera m'mudzi mwa Mankhumba mudera la mfumu Timbiri m'bomalo akuti anagwirira mwana wake wa mkazi wa zaka zinayi atapezerapo mwayi pa kusakhalapo kwa mkazi wake.

Mneneri wa polisi ku Nkhata Bay, Ignatious Essau, adati pakati pa 2 ndi 5 Novembara chaka cha 2015, mkazi wa bamboyu anachokapo kwa kanthawi ndikumusiya mwanayo ndi bambo ake omwe anamugwiririra.

“Mayiwo atabwerako, anaona kuti mwana wawo wa mkazi akuvutika kukhala pansu ndipo atafunsa mwanayo, anatchula

momveka bwino kuti bambo ake ndi amene amugwiririra,” anatero a Essau.

Mneneri wa polisiyo adafotokozanso kuti nkhanayi idakatulidwa ku polisi komwe wovulalayo adatumizidwa ku chi-patala cha boma la Nkhata Bay. Atamuyeza, zinaululika kuti mwanayo analidi atagwiriridwa.

Padakali pano woganiziridwayo ali kundende ya Nkhata Bay komwe akudikirira kukaonekera kubwalo la milandu kuti akayankhe mlandu wogwiririra womwe ngati adzapezeke wolakwa atha kudzalandira chilango chokhala kundende ndi kugwira ntchito ya kalavula gaga kwa zaka 14.

Pasanathe miyezi iwiri, bwalo la milandu la Nkhata Bay linaweruza anthu asanu pa milandu yogwiririra; zinthu zomwe Magistrate Ngosi anena kuti ndi zodetsa nkhwama poganizira kuti opezeka olakwa akupatsidwa zilango zokhwima.

“Ndi zomvetsa chisoni kuona kuti ngakhale bwalo la milanduli likupereka zilango zokhwima kwa anthu opezeka olakwa pa milandu yogwiririra, opalamula milanduyi akuchulukirabe m’bomali,” adatero Ngosi.

Iye adatinso ndi zomvetsa chisoni kuti anthu omwe akadakhala pa tsogolo poteteza ufulu wa ana ndiwo akuuphwanja.

Pamene a Blackson Mhone akudikila mulandu wawo, bwalo loweluza milandu ku Nkhata Bay linagamula kuti Harrington Phiri, wa zaka 22 zakubadwa, akakhale ku ndende zaka 7 kamba kopezeka olakwa pogwiririra mwana wa sukulu wa sitandade 8.

Bwaloli lidamva kuti mu Okutobala chaka cha 2014, wolakwayo adachita chibwenzi ndi mtsikana wa zaka 15 zakubadwa yemwe anali sitandade 8 pa imodzi mwa sukulu

za pulaimale m'bomalo zomwe zidapangitsa kuti mtsikanayo asakhale ndi chidwi chopitiliza maphunziro ake.

A Phiri akuti amalumikizana ndi agogo a mtsikanayo kuti amunyengerere mtsikanayo kuti amukwatire, koma izi sizin-asangalatse bambo a mtsikanayo makamaka ataona mwana wawo wa mkazi akutuluka m'nyumba ya Phiri tsiku lina.

Bambo anakwiya kwambiri ndipo anawatengera onse awiri ku polisi ya Nkhata Bay komwe anakadandaula zomwe zinapangitsa kuti Phiri atsekeredwe ndikuimbidwa mlandu wogwirira.

Ku bwalo la milandu, a Phiri adakana mlandu wogwiririra koma boma kudzera mwa oyimira boma pa milandu a polisi motsogozedwa ndi Inspector Evance Kamtukule adawonetsa mboni zitatu zomwe zidapereka umboni wotsutsa wolakwayo ndipo bwaloli linamupeza wolakwa pa mulanduwu.

Podandaula, a Phiri adachonderera oweluzza mulandu kuti amukhululukire ndipo adapempha bwalo kuti limupatse chilango chosakhala m'ndende.

“Ndikuchonderera bwaloli kuti lisanditsekere ku ndende chifukwa kutero kungasokoneze tsogolo langa chifukwa mayi anga ndi hule ndipo ndikufuna ndikapitilize maphunziro,” adatero Phiri.

Koma Inspector Kamtukule adapempha bwalo kuti limupatse chilango chokhwima kuti achenjeze ena.

“Kupempha kwanga kuti bwalo la milandu lipatse wolakwayu chilango chokhwima kuti ena atengepo phunziro po-peza milandu yogwiririra ikuchuluka m'bomali,” adatero Inspector Kamtukule.

Woweruza mulanduwu, a Billy Wankaya Ngosi, adagamu-
la kuti Harrington Phiri akakhale m'ndende miyezi 84 akug-
wira ntchito ya kalavula gaga chifukwa chogwiririra.

Harrington Phiri amachokera m'mudzi mwa Chimeji mu
dera la mufumu Mtwalo m'boma la Mzimba.

Milandu yambiri yokhudzana ndi chikhalidwe cha ana
imayendetsedwa ndi lamulo la Penal Code ku Malawi. Ndon-
domeko ya chilango imatanthauzira mawu oti mwana ngati
munthu wosakwanitsa zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu (18).

Lamulo la Penal Code monga taonera m'mitu yapitayi
limatanthauzira “**zogonana**” ngati **kugonana** kwina ko-
sakhuzza kulowetsa chiwalo cha umuna monga kuyika chi-
walo cha umuna kukamwa kapena ku mbuyo kochitila
chimbuzi; kuseweretsa maliseche; kugwirana maliseche,
kumbuyo kapena mabere; kuzunza munthu wina m'thupi
kapena m'maganizo pofuna kudzutsa chisangalalo cha
kugonana ndi chisangalalo; ndi zonyansa zina zogonana;

“**Kugonana koletsedwa**” kumaphatikizapo kugonana,
kugonana kumbuyo, kuseweretsa maliseche, kuyamwa mali-
seche, kugonana ndi nyama, kuzunza munthu wina m'thupi
kapena m'maganizo pofuna kudzutsa chisangalalo cha kugo-
nana ndi chisangalalo; ndi zonyansa zina zogonana ndi cho-
linga chofuna kugonana kapena kukondweretsa munthu ali
yense amene angawone chithunzicho; “**zakuthupi**”; kupha-
tikiza (a) chinthu; (b) chithunzi chowonekabe chamtundu uli-
wonse, kaya ndi chojambula, chojambula ndi pensulo kape-
nanti, komanso chosindikizidwa kapena ayi; (c) chithunzi
chosuntha. Kaya yopangidwa kuchokera ku kanema, tepi ya
kanema kapena njira ina, kapena (d) chounika;

“Zinthu zonyansa” zikutanthauza zinthu zomwe: (a) Kufotokoza, kufotokoza, kapena kuchita zinthu zokhudzana ndi kugonana, kugwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo kapena kuledzera, umbanda, nkhanza kapena chiwawa, kapena zochitika zonyansa, m’njira yomwe ingakhumudwitse munthu wa mkulu; (b) akuwonetsa munthu (kaya akuchita zogonana kapena ayi) yemwe ali, kapena mwachiwonekere, mwana wosakwanitsa zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi m’njira yomwe ingakhumudwitse munthu wa mkulu wololera: (c) akufotokoza, chikuwonetsa, kufotokoza, kapena kuchita zogonana za mtundu uliwonse pakati pa munthu ndi nyama.

M’malamulo, munthu ali yense amene wagonana ndi mwana adzakhala wopalamula ndipo adzakhala m’ndende zaka khumi ndi zinayi.

Ngati mulanduwo wachitika mowopseza, wopalamulayo ayenera kukhala ku ndende kwa zaka makumi awiri ndi chimodzi.

“Moopseza” amatanthauza kuti oimbidwa mlandu anali ndi chida chilichonse choopsa kapena choyipa kapena chida kapena adanama kuti ali ndi zida.

Wozengedwa mulandu anali ndi munthu wina kapena an-thu ena; wozengedwa mulandu chifukwa cha zochita zake kapena kuvulaza, kuononga kapena kuyika moyo wa wo-zunzidwayo pa chiopsezo; wozengedwa mulandu amachita chinthu chomwe chingaononge kapena kuchititsa manyazi wozunzidwayo; kapena wozengedwa mulandu akuopseza kupha wozunzidwayo; wozengedwa mulandi ndi kholo lomupeza.

Kholo longomusunga, mphunzitsi, ndi womulera kapena ndi munthu amene ali ndi utsogoleri kapena udindo wa mwa-nayo kapena ndi munthu amene mwanayo akukhala naye monga gawo la banja la woimbidwa mlandu.

Munthu aliyense amene, kaya pagulu kapena mwanseri, atenga mwana kuti achite zogonana ndi iye kapena ndi munthu wina; kapena wachita zogonana ndi munthu yemwe ndi mamuna kapena mkazi mnzake pamaso pa mwana, adzakhala wopalamula ndipo adzakhala m'ndende zaka khumi ndi zinayi.

Munthu aliyense amene, ali ndi cholinga cholakwira lamulo, kugulitsa, kapena kuonetsa zinthu zolaula kwa mwana, adzakhala wopalamula ndipo ayenera kukakhala kundende zaka zisanu ndi ziwiri.

Munthu aliyense amene amayambitsa kapena kuguli-ra mwana aliyense, kapena ndi kholo kapena woyang'anira mwanayo amalola mwanayo kutenga nawo mbali mu zosangalatsa zili zonse zogonana; chomwe chili choopsa ku moyo kapena kusokoneza thanzi la mwanayo, thupi komanso kusasamalidwa bwino kwa mwanayo, akhale wopalamula ndipo azilipira chindapusa cha MK 100, 000 komanso kukakhala kundende zaka zisanu ndi ziwiri.

Ngati munthu wopezeka ndi mulandu wolola kuti mwanayo atenge nawo mbali pa zosangalatsa zili zonse zogonana ndi amene ali ndi chilolezo choperekedwa ndi lamulo loletsa zosangalatsa za anthu onse kapena pansu pa lamulo lina lililonse loyenerera, bwalo loweluzza milandu likhozanso kulamula kuti alandidwe chilolezocho kapena kuyimitsidwa kwa nthawi yomwe bwalo la milandu lingaganize kuti ndikoyenera.

Wozengedwa mulandu sadzaloledwa kuziteteza pa mulanduwu ponena kuti samadziwa kuti mwanayo anali wa zaka zosakwana khumi ndi zisanu ndi chimodzi, kapena amakhulupirira kuti mwanayo sanali pansu pa msinkhu umenewo.

MUTU WA CHIKHUMINDI CHIWIRI

KUTENGA MBALI

Mphunzitsi wa mkazi ku Ntchisi anadabwitsa anthu pamene anabweretsa poyera nkhani ya mtsikana wa zaka 14 zakubadwa wapa sukulu ya pulaimale ya Kalema yemwe amagwiriridwa ndi amalume ake. Iye anayetsa kutengera nkhanayi kwa akuluakulu osiyanasiyana.

Mphunzitsiyo, Maria, adawona khalidwe la chilendo mwa mtsikana wina wa sitandade 6 (dzina sititchula) ndipo atakumana naye, mtsikanayo adaulula kuti amagwiriridwa mobwerezabwereza ndi amalume ake nthawi zonse azakhali ake akachoka.

“Mtsikanayo samatha kumvetsera mkalasi; amakhala ndi maganizo nthawi zonse ali mkalasi. Ndinadziwa kuti anali ndi vuto. Anandiululila kuti amalume ake akumugwiririra komanso kuti ali ndi mimba. Ndinakwiya kwambiri,” adatero Chawanda pamene anapereka umboni pa mulanduwo ku bwalo loweluza milandu.

Mphunzitsi wa mkaziyu adati atamva za nkhanza zomwe msungwanayu amakumana nazo ku nyumba kwake,

adatengera nkhaniyi kwa mphunzitsi wa mkulu komanso ku gulu la amayi apa sukuluyi omwe onse adati sangathane ndi nkhaniyi chifukwa woganiziridwayo ndi chigawenga.

“Ndinasweka mtima kwambiri atandiuza poyera kuti woganiziridwayo ndi chigawenga ndipo akhoza kuthana nawo ngati atazindikira kuti akuyendetsa nkhaniyo. Ndinamva chisoni kwambiri koma ndinatsimikiza mtima kuti ndipitirirebe chifukwa ndimadziwa kuti tsogolo la mtsikanayo liku-wonongeka tikayima pambali ndi kuonera,” adatero mphun-zitsiyo.

Kenako Chawanda adatengera nkhaniyi ku bungwe lina la achinyamata la m’bomalo kenaka adapita ku bungwe la Plan Malawi lomwe idamuthandiza kutengera nkhaniyi ku polisi kuti alowererepo.

“Zinali zomvetsa chisoni kwambiri kuti ngakhale nthambi za boma zomwe udindo wawo ndi kuteteza ana sizinadathe kuthandiza ngakhale ndinanenapo za nkhaniyi. Zonse zin-anditsalira ine ndipo ndinali wokonzeka kuchitapo kanthu chifukwa ndimkafuna kuona mtsikanayo akupulumutsidwa,” adatero.

Chawanda adati patatha masiku angapo akusaka chilungamo pa nkhaniyi, mtsikanayo adakakamizidwa kuchot-sa mimba ali ku nyumba. Anamupatsa mankhwala ena ake omwe anakakamizika kuwameza ndipo ena anamuika mali-seche ake.

“Izi zinandikwiyitsanso kuposa kale, mtsikanayo adadut-sa mu gehena. Misozi yake inanditsimikizira izi pamene amandifotokozera. Adapatsidwa mankhwalawa cha m’ma 9 koloko m’mawa koma mimba idachoka cha m’ma 5 madzu-

lo ali yekha m’nyumba. Ndikumva kuti dokotala wina wake anabwera kudzamuchita izi, ndikanakonda nditadziwa dzina lake,” adatero mphunzitsiyo.

Mphunzitsiyo adati ndi okondwa kuti nkhanayi ili ku bwalo loweluzza milandu koma akuda nkhwawa kwambiri ndi chitetezo cha mtsikanayo chifukwa sanasamuke.

“Tangoganizani kuti iyeyo ndi amene amatengera chakudya kwa amene amati ndi amalume ake omwe ali m’ndende ya Ntchisi. Kodi ichi ndi chilungamo? Kodi mtsikanayo akukhudzidwa bwanji m’maganizo ake? Ndili ndi mantha kuti kulephera kumuchotsa pa nyumbapo kusokoneza chilungamo chifukwa chili chonse chitha kumuchitikira,” adatero.

Mkati mokamba mulanduwa, mtsikanayo anali ndi vuto lofotokoza za vutolo. Amangonena kuti adandigwiririra kangapo. Aphunzitsi ake adabwera ngati mboni yayikulu pa mulanduwa womwe amalume amaukana. Panali vuto lopeza malo otetezeka bwino oti mtsikanayo akakhaleko popeza mabungwe odalirika samafuna kumuthandiza.

Mkulu wa bungwe la Ntchisi Organisation for Youth and Development (NOYD), yemwe nakhala akuthandiza Maria pa nkhani ya mtsikanayo, dati apolisi ndi bungweli adagwirizana kuti atengere mtsikanayo kwa makolo ake omubereka ku Mulanje.

“Zonsezi zikuchitika makolo ake ali moyo koma ndi kukhulupirira kuti iwo sakudziwa momwe mwana wawo alili kuno ku Ntchisi. Tikulakalaka akadakhala nawo kuti amuteteze. Ndiye tikumuperekeza ku Mulanje poti wapereka kale umboni ku bwaloli,” adatero Kalumo.

Ngati mukufuna kuteteza mwana wanu ku nkhanza zogonana, uwu ndi mwayi wanu wopanga malo otetezeka komanso othandiza aliyense m’banja mwanu. Ana amakhala otetezeka nthawi yomweyo makolo ndi owalera akapeza nthawi yophunzira za kugwiriridwa.

Ziopsezo za nkhanza zogonana

Ndilankhula za zinthu zomwe zimayika munthu pa chiwopsezo chogwiririra mwana. Ndikambanso za zinthu zoteteza kuphatikizapo zimene banja lingachite kuti banja likhale lotetezeka. Zinthu zoteteza ndi zomwe zimamanga banja lanu.

Makolo ndi olera ana amene amalonjeza kulankhula mwamsanga akakhala ndi nkhwawa, m’ malo modikira kupeza umboni wakuti wavulazidwadi, ndi ofunika kwambiri pa chitetezo cha mwana.

Makolo ayenera kudziwa zizindikiro ngati “mwayi wopewera” mwayi woti makolo a chikondi azindikire zoposa zomwe zingachitike ndi kuchitapo kanthu poteteza ana. Kumbukirani, kupewa ndi kothandiza kwambiri kuposa kulanga wopalamula mulandu.

Makolo ayenera kulimbikitsa njira zokambirana ndi mwana, wa chinyamata, kapena wa mkulu, momasuka za makhalidwe ogonana kapena nkhwawa zawo, kukambiranako siku-chitika kamodzi kokha.

Ali yense m’banjamo adziwe kuti ndi bwino kufunsa mafunso. Ndikofunikira kuti akuluakulu akhazikitse njira zoti ali yense pa banjapo azimasuka pokambirana nkhani zokhudza machitidwe ogonana omwe ali abwino komanso za nkhanza

zogonana.

Makolo ayenera kumvetsetsa za kakulidwe kabwino ka ana komanso machitidwe ogonana omwe angakhale odetsa nkhawa kwa inu monga kholo.

Makolo ayenera kuphunzira zizindikiro zomwe mwa-na amene wavulazidwa ndi nkhanza zokhudza kugonana komanso zizindikiro zomwe munthu wa mkulu kapena wa chinyamata amene akuchita nkhanza zogonana amaonetsa. Nkhawa zanu zikhoza kukhala zokhudzananso ndi makhalidwe monga kuwonetsa mwana zolaula.

Makolo ayenera kuphunzitsa ana mayina oyenerera a ziwalo za thupi ndi zimene ayenera kuchita ngati wina ayesa kuzigwira mwa kugonana. Kumbukirani kuti ana a ang'ono ayenera kudziwa kuti palibe amene ali ndi ufulu wokhudza maliseche awo (kupatulapo pa zifukwa za chipatala) ndipo kuti iwo sayenera kugwira maliseche a wina ali yense.

Mabanja ayenera kukambirana ndi kukhazikitsa malamulo omveka bwino amomwe achibale komanso akuluakulu azichezera kapena kuyang'anira ana (mwachitsanzo, osamukakamiza mwana kukumbatirana kapena kupsopsona wina popatsana moni kapena kutsanzikana, m'malo mwake akhoza kugwirana chanza).

Ngati mwana samasuka ndi munthu wina wa mkulu kapena wachinyamata ndiye kuti inuyo kapena munthu wina wa mkulu muyenera kumudziwitsa munthuyo (mwachitsanzo, muuzeni kuti simukufuna kuti mwana wanu azikhala pa miyendo pake).

Mwana akamakula, malamulo a m'nyumba amafunikanso kusintha (mwachitsanzo, kugogoda pa khomo asanalowe

m'chipinda cha wachinyamata).

Onetsetsani kuti palibe m'banja mwanu amene ali yekhayekha. Dziwani munthu m'modzi kapena angapo othandizira ali yense m'banjamo.

Kafukufuku akusonyeza kuti chimodzi mwa zinthu zofunika kwambiri pa kulimba mtima kwa mwana (kutha kukhala bwino atadutsa mu zovuta) ndikuti anali ndi wina woti al-ankhule naye ndi kumuululira za kukhosi.

Ngati wina ali “wabwino kwambiri modabwitsa” muyenera kudzifunsa mafunso enanso mwana wanu sangakhale wotetezeka kwa bwenzi kapena wachibaleyu. Kukhulupirira kopanda malire sikungateteze ana ku zoipa.

Samalani mwanzeru ndi anthu omwe ali ndi mwayi wopeza ana anu. Samalani ndi anthu amene akulabadira za ana anu ndi mabwenzi awo. Musanyalanyaze chikayiko chilichonse chomwe mungakhale nacho ponena za anthu amene amasonyeza chidwi pa mwana wanu.

Makolo ayenera kudziwa komwe angapeze thandizo mu dera lawo. Dziwani za mabungwe omwe ali m'dera lanu, gulu la a chitetezo, mabungwe omwe siaboma komanso nthambi ya boma yosamalira anthu. Dziwani yemwe mungamuimbire foni kuti muwadziwitse ngati mwamva kuti mwana wagwir-iridwa.

Ngati mukhudzidwa ndi khalidwe la kugonana la kholo, msuweni, mbale, nzanu, kapena m'nansi, samalani mokwan-ira kuti mulankhule nawo. Ngati mukukhudzidwa ndi malingaliro anu kwa ana funani chithandizo.

Ndikofunika kwambiri kuti kholo lililonse lidziwe zizindikiro zosonyeza kuti ana ndi achinyamata atha kukhala kuti

akumana ndi nkhanza zogonana. Nthawi zambiri ana amationetsa m'malo motiuza kuti pali chinachake chimene chawakhumudwitsa. Pakhoza kukhala zifukwa zambiri zosinthira khalidwe lawo, koma ngati tiwona zizindikiro zodetsa nkhwawa, imeneyi ndi nthawi yopeza thandizo kapena uphungu.

Zizindikiro zina zomwe mukuyenera kuziyang'anira zimaphatikizapo pamene mwana akuchita zosewera mosonyeza mchitidwe wogonana. Mwanayo akulota maloto oopsa komanso amavutika kugona kapena amadzipatula, amakamira zinthu kwambiri kapena wayamba zinsinsi.

Kusintha kwa umunthu kwa dzidzidzi, kusinthasinthwa kwa maganizo ndi kuoneka ngati wosatetezeka; kubwerera ku makhalidwe a umwana, mwachitsanzo kukodzera pogona; mantha osaneneka a malo ena ake kapena anthu; kukhala ndi mkwiyo; kusintha kwa kadyedwe; kutchula mawu atsopano olaula a ziwalo za thupi mosadziwika komwe waziphun-zira; kukamba za bwenzi la tsopano la chikulire komanso kupezeka ndi ndalama kapena mphatso zosadziwika bwino komwe zachokera kapena kudzipweteka pozicheka, kuz-iwotcha kapena mu njira zina ndi zizindikiro zina zomwe muyenera kuziyang'anira.

Ndikofunika kuchita chidwi ndi zizindikiro za thupi la mwana wanu, monga, zilonda zosadziwika bwino kapena mabala ozungulira maliseche kapena mkamwa, matenda opatsirana pogonana, ndi mimba.

Mwanayo sangafune kukhala yekha ndi mwana winawake kapena wachinyamata winawake.

Chizindikiro chili chonse sichikutanthauza kuti mwana

adachitiridwa nkhanza kapena akugwiridwa, koma kupeze-ka kwa zizindikiro zingapo kumasonyeza kuti muyenera kuyamba kufunsa mafunso ndikuganizira zopeza thandizo.

Kumbukirani kuti zina mwa zizindikirozi zimatha kuwonekera nthawi zina za kupsinjika maganizo monga: Pachisudzulo, imfa ya wa chibale kapena chiweto, mavuto ku sukulu kapena ndi abwenzi kapena zochitika zina zokhumudwitsa.

Zizindikiro za ku thupi za nkhanza zogonana ndizosowa, komabe, ngati muwona kupweteka ku maliseche; kuchucha kapena kutuluka magazi ku maliseche, kuthako kapena pakamwa; kupweteka kosalekeza pokodza ndi matumbo; ndi kukodzedwa kapena kuchita chimbudzi muzovala, tengerani mwana wanu kwa dokotala. Dokotala wanu akhoza ku-kuthandizani kumvetsetsa zomwe zikuchitika ndikuyeza ma-tenda opatsirana pogonana.

Zizindikiro zosonyeza kuti munthu wa mkulu akugwiritsa ntchito ubale wake ndi mwana pa zifukwa zogonana sizingakhale zoonekeratu. Titha kukhala osamasuka ndi momwe amasewerera ndi mwana, kapena kuwoneka ngati amawakondera nthawi zonse ndikupangitsa kuti azikhala okha.

Pangakhale chifukwa chodetsa nkhwawa pa khalidwe la munthu wa mkulu kapena wa chinyamata ngati: akana kulola mwana kukhala pa yekha kapena kupanga zisankho pa nkhani zomukhudza.

Khalani ndi chidwi ngati munthu wa mkulu akukakamira kupereka chikondi chakuthupi monga kupsopsonana, kukumbatirana kapena masewera okhudzana ngakhale pamene mwanayo sakufuna, ngati wa mkuluyo ali ndi chidwi chodab-

witsa pa kuntha msinkhu kwa mwana kapena wa chinyamata kapena akuumirira kukhala yekha ndi mwanayo popanda zosokoneza.

Khalani ndi chidwi chapadera ngati munthu wa mkulo am-athera nthawi yake yambiri yopuma ndi ana ndipo alibe chidwi chocheza ndi anthu amsinkhu wake kapena amadzipereka mokhazikika pa ntchito yolera ana mwaulere kapena kupita ndi ana kokacheza yekha usiku wonse.

Taonapo nkhani zambiri za amalume omwe amagulira ana mphatso za mtengo wapatali kapena kuwapatsa ndalama popanda chifukwa. Khalani ndi chidwi ndi kuletsa makhalidwe amenewa.

Ena, nthawi zambiri amalowera ana kapena achinyamata pomwe akusamba kapena amakonda mwana wina modabwitsa, zomwe zimawapangitsa kudzimva kukhala ‘apadera’ poyerekeza ndi ena m’banjamo kapena kumotola mwana winawake.

Monga kholo kapena wolera mwana, muyenera kudzi-wa kuti ana amadutsa m’magawo osiyanasiyana akamakula, komanso kuti kuzindikira kwawo komanso chidwi chawo pa nkhani zogonana zimasintha akamachoka paukhanda kupita ku ubwana, kenako kutha msinkhu ndi kufika pa unyamata.

Mwana aliyense ndi munthu payekha ndipo amakula mwa njira yakeyake. Komabe, pali mitundu ya chidwi yovomereze-ka yokhudzana ndi msinkhu wa mwana ndi kakulidwe kake.

Nthawi zina ana amakhala ndi chidwi chofufuza zinthu ndi ana ena a msinkhu wawo. Zingakhale zovuta kusiyantsa pakati pa kufufuza koyenerera za kugonana ndi zizindikiro zochenjeza za khalidwe loipa. Nthawi zina tingafunikire ku-

fotokozero ana chifukwa chimene tingakonde kuti asapitirize ndi khalidwe linalake.

Uwu ndi mwayi wolankhula nawo za kudzisunga iwo eni ndi ena komanso kuwadziwitsa kuti ndinu munthu amene mungamvetsere. Ana olumala akhoza kukula mosiyanasiana, malinga ndi ulumali wawo, ndipo akhoza kukhala pa chiopsezo cha nkhanza.

Mwachitsanzo, ana omwe ali ndi vuto lophunzira amatha kuchita zinthu zosemphana ndi msinkhu wawo. Chisamaliro chapadera chingafunikire pophunzitsa ana oterowo za kakulidwe kawo komanso zogonana ndi kuwatsimikizira kuti angathe kulankhula za nkhaŵa zilizonse zimene ali nazo.

Ndikofunika kuzindikira kuti ngakhale kuti anthu ochokera m'madera osiyanasiana amayembekezera zosiyana pa khalidwe lovomerezeka kwa ana, nkhanza zogonana zima-chitika m'mitundu ndi zikhalidwe zonse.

Kumbukirani kuti mwana ali yense amakula pa liwiro lake ndipo simwana aliyense amene angasonyeze makhalidwe omwe afotokozedwa pansipa.

Zizindikiro zina zosonyeza kuti ana a zaka za pakati pa 0 ndi 5 za kubadwa akuchitidwa nkhanza zogonana ndi awa: kugwiritsa ntchito chinenero cha chibwana 'chogonana' polankhula za ziwalo za thupi; kufunsa m'mene makan-da amapangidwira komanso kumene akuchokera; kugwira kapena kusiona maliseche awo; ndikuonetsa ndikuyang'ana ziwalo zawo zobisika.

Sikawirikawiri komwe anawa: amakambirana za kugonana kapena kulankhula zolaula; kugonana ndi ana ena; ndikuwonetsa machitidwe ogonana ngati akuluakulu kapena chid-

ziwitso.

Pa nkhani ya ana a msinkhu wa zaka 6-12, nthawi zambiri amafunsa mafunso okhudza kusamba, mimba ndi makhalid-we ena ogonana.

Amayesera ndi ana ena, nthawi zambiri posewera, kup-sopsonana, kugwirana, kusonyeza ndi kusewera mwa chit-sanzo monga amayi ndi abambo, kapena madotolo ndi ana-mwino komanso kuseweretsa maliseche awo mwa chinsinsi. Ana samakonda kuseweretsa maliseche pa gulu kapena ku-wonetsa anthu akuluakulu monga kugonana kapena kudzi-wapo kanthu.

Achinyamata amafunsa mafunso okhudza maubwenzi ndi machitidwe ogonana; kugwiritsa ntchito mawu okhudza zo-gonana pokambirana pakati pawo za kugonana. Amasewer-etsa maliseche awo kapena kuyesa kugonana ndi achinyamata amisinkhu wawo. Samakonda kuseweretsa maliseche pa gulu kapena kugonana ndi ana a ang'ono kapena akuluakulu.

Chimodzi mwa zinthu zovuta kwambiri kuti makolo az-indikire ndi chakuti mwana wawo akhoza kuvulaza kapena kugwiririra mwana wina. Munthawi imeneyi, kholo silikhu-lupirira, limakhala lodzidzimuka komanso lokwiya ndi zochitika za chilendozi.

Ngati sipachitika kanthu mwamsanga ndi mwachidwi, zitha kusokoneza banja lonse. Pa chifukwachi, ndi pofuni-ka kukaonana ndi munthu wina kuti akupatseni malangizo a zimene mungachite mukangokayikira kuti chinachake chal-akwika.

Uthenga wabwino ndi wakuti chithandizo chofulumira kwa mwanayo kapena wa chinyamata ndi banja lawo chin-

gathandize kwambiri.

Pali umboni wakuti ana omwe amalandira thandizo mwa nsanga amakhala ndi mwayi wochulukira woti khalidwe loipa-lo lisakhazikike. Ndikofunika kukhala tcheru ndi zizindikiro zochenjeza kuti chinachake sichikuyenda bwino.

Ngati zili choncho, kumbukirani kuti simuli nokha. Makolo ena ambiri anakumanapo ndi zofananazo ndi zomwe mwakumana nazozo, ndipo kuti mwanayo ndi banjalo anazindikira kuti thandizo limene analandira linamanganso miyoyo yawo. Chinthu choyamba ndicho kuona kuti zingakhale zothandiza kukambirana ndi munthu wina.

Ngati mukhudzidwa ndi khalidwe la kugonana kwa kholo, msuweni, mchimwene wanu, m'nzanu, kapena woyandikana nawo nyumba, muyenera kulingalira za kulankhulana ndi apolisi kapena oteteza ana m'dera lanu; atha kuchitapo kanthu ngati kuli koyenera. Ngati mwasankha kusatero, samalani mokwanira kuti mulankhule ndi munthu amene khalidwe lake likukudetsani nkhawa.

Ana atatu mwa anayi alionse amene amagwiriridwa sauza aliyense za izi ndipo ambiri amabisa izi moyo wawo wonse. Ogwiririra nthawi zambiri amakhala anthu omwe timawadziwa, ndipo akhoza kukhala anthu omwe timawakonda. Ndipo ana osachepera asanu ndi atatu mwa ana khumi alionse amene amagwiriridwa amadziwa amene amawachitira nkhanzawo.

Ndi achibale kapena abwenzi, oyandikana nawo kapena olera ana. Ambiri ali ndi maudindo m'maderamu. Anawa amalephera kuulula za nkhanza maka wochita nkhanzayo akakhala m'bale wapafupi.

Nthawi zambiri ana amationetsa m'malo motiuza kuti pali

chinachake chimene chawakhumudwitsa choncho kudziwa zizindikiro ndi kofunika kwambiri. Komabe, ana amaonetsa zizindikiro zosonyeza kuti chinachake chikuchitika.

Uthenga wawo sungakhale womveka bwino ndipo sanga-khale ndi mawu ofotokozera zomwe zikuwachitikira. M'mene akuluakulu alandirira uthengawu ndi kofunika kwambiri pa chitetezo cha mwanayo.

Chitani kanthu mosamala komanso mwa changu ngati mukuganiza kuti mwana akuyesera kukuuzani za nkhanza zogonana. Apolisi ndi ma bungwe oteteza ana ali ndi ndondomeko yogwirira ntchito limodzi pa mulandu womwe akuganizira kuti mwana wagwiridwa. Iwo ndi odziwa bwino ntchito imeneyi ndipo adzachita zinthu mokhudzidwa ndi mwanayo ndi banja lake.

Ngati mwana amakukhulupirirani mokwanira kuti akuuze-ni za nkhanza, muyenera kukumbukira kuti nthawi zambiri sanama pa zinthu zoterezi. Ngakhale zili zovuta kukhulupirira kuti munthu amene timamukhulupirira kapena amene timamukonda angathe kugwiririra mwana, ndi zokayikitsa kuti mwana anganene za bodza zokhudza kugonana ngati munthu wa mkulu.

Zinthu zambiri zimatha kumuletsa kulankhula nkhaniyi. Pamafunika kulimba mtima kwambiri kuti alankhule za nkhanza. Zonena za mwana kuti nkhanza zakugonana sizinachitike (pamene zidachitikadi), kapena kusintha zomwe anaulula za nkhanza kumachitika kawirikawiri.

Nthawi zina mwanayo amasinthasintha nkhani ya zomwe zinachitika pakapita nthawi. Iyi ndi njira yodziwika bwino yowulula ndipo siyenera kukayika nkhani yawo. Ndi pofuni-

ka kuti aziona kuti akuthandizidwa. Osatsutsa zonena zawo kapena kuwatsekereza kuti alankhule za izo.

Ngati mwanayo akulankhula nanu za nkhaniyi, musakwiye. Khalani odekha ndi okhazikika. Mukapsa mtima, mwanayo angaganize kuti mumulanga. Izi zidzachitira ubwino wozunzayo yemwe adachenjeza mwanayo kuti asanene.

Onetsetsani kuti mwanayo akudziwa kuti mumamukonda komanso kuti sanalakwe ndipo pitirizani kumuza. Mwanayo ayenera kuona kuti akuluakulu amawakhulupirira ndipo akuchita zonse zomwe angathe kuti amuteteze. Onetsetsani kuti mwanayo akudziwa kuti analondola pokudziwitsani za nkhaniyi komanso kuti ndinu okondwa kuti anabwera kwa inu.

Pamene nkhanzayo yadziwika, akuluakulu ayenera kuwunikira vutolo moona mtima, kuteteza mwanayo mu njira iliyonse m'mene zingakhalire ndi kuonesetsa kuti wogwirirayo agwidwe. Chitani zomwe zikufunika kuti muteteze mwanayo ku zovuta zina. Pezani thandizo kuchokera kwa akatswiri omwe angakuthandizeni kukutsogolerani ku chitezezo ndi machiritso. Ana angathe kuchira akagwiridwa. Ndizovuta kwambiri kumva kuti munthu amene mumamukonda wavulazidwa mwanjira yotere koma kuwathandiza kuti achire ndikofunikira.

Monga kholo, muyenera kudziwa kuti mwanayo amaopa kuti munthu amene wamuchitira nkhanzayo angakane kapena kuvulaza iwo kapena amene amawakonda. Iye adzachitamba kuti palibe amene angamukhulupirire. Amakhala ndi nkhwana komanso osutsika m'maganizo. Sadziwa amene angamukhulupirire. Zotsatira zake, iye amafuna kuti ateteze kapenanso akonde munthu amene adamuchitira nkhanza.

Amanong'oneza bondo kuti adawulula zomwe zidawachitikira (atha kukana zomwe zidawachitikira).

Ndaphunzirapo kuti ana nawonso amakhulupirira kuti ndi amene anachititsa kuti achitiridwe nkhanza. Amazimva kulakwa pokhumudwitsa abale awo powauza za nkhaniyi komanso amachita manyazi ngati anamva kukoma pochitidwa nkhanzayo.

Ndi zomvetsa chisoni kuti nthawi zambiri m'Mala-wi muno, banja lonse limakhudzidwa pamene mwana wachitiridwa nkhanza ndi wa chibale.

Nthawi zambiri, thandizo la akatswiri akunja limafunikira pothana ndi vuto la malingaliro pa banja komanso kuthandiza kuchira kwa munthu aliyense. Ululu umene timakumana nawo ukhoza kuphatikizapo kusagwirizana ndi kusokonezeka kwa maganizo.

Timamva chisoni kwambiri ndi zimene zinachitidwa kwa mwanayo, pamene tikukhalabe ndi chikondi ndi chisamaliro kwa wachibale amene anachita nkhanzayo.

Makolo oteteza ndi okonda ana amakwiwira yemwe wavulaza mwana wawoyo pa zomwe wachita, posakhulupirika, popusitsa komanso powasokoneza. Nthawi zambiri makolo amakwiwira mwana chifukwa chosawulula msanga.

Ena amadziimba mulandu chifukwa chosazindikira zomwe zinali kuchitika mwansanga kuti ateteze mwanayo (ngakhale wolakwayo atachita zonse zomwe akanatha kuti asunge chinsinsi).

Makolo ambiri kapena osamalira amada nkhanza ndi zot-satira za nkhanzazo komanso tsogolo la banja lawo.

Azimayi ndi ana amamva chisoni chifukwa cha kutaya moyo umene anali nawo, kapena kuganiza kuti anali nawo, asanadziwe za nkhanzazo.

Monga makolo oteteza ndi okonda ana awo, mumafunikiranso chithandizo. Kulumikizana ndi anthu omwe mungawafotokozere za kukhosi kwanu kungakuthandizeni kuthana ndi zoopsa komanso zovuta zomwe munakumana nazo.

Munthu amene wagwiririra mwana ayenera kuyimbidwa mulandu ndi kupeza thandizo la akatswiri. Apolisi akumaloko kapena ogwira ntchito zoteteza ana nthawi zambiri amadzi-wanjira zoyenera kutsata pothandiza. Ngati mwasankha kusalumikizana nawo, ndipo ngati kuli kotetezeka, ganizirani kulankhula mwachindunji ndi wolakwayo.

Ngati mwalimba mtima kuti mulankhule ndi wolakwayo, chonde fufuzani nkhaniyo mopanda kuweruza komanso ku-kangana. Zimenezi zingathandize kuchepetsa chitetezo cha munthuyo. Muyenera kukhala achindunji pa zomwe zimak-ukhudzani ndikumufotokozera zomwe mukuchita pa izi. Funsani mafunso osavuta komanso achindunji.

Mudziwitseni munthuyo kuti pali thandizo; anthu atha kukhala ndi moyo wopanda nkhanza potenga udindo wawo pa zolakwa zomwe adachita, kuvomera zotsatira za zochi-ta zawo, ndikuvomera kuti asinthe ndikulandira chithandizo cha padera.

Ngati mukumva, muuzeni munthuyo kuti mumamukonda. Thandizo la chikondi lingakhale chinthu chofunika kwambiri kuti wina atenge udindo, kuvomera zotsatira zake ndi kulandira chithandizo. Kukambirana nthawi zambiri kumafunika kuchitika kangapo. Pezani wothandizana naye

amene mungapiteko kuti akuthandizeni.

Chonde dziwani kuti, pamene nkhanzayo yavumbuluka, munthu wolakwayo matha kumukwiyira mwanayo poulu-la. Amakhala odzida kwambiri ndipo angafune kudzivula-za kapena kudzimvera chisoni chifukwa cha zoipa zimene anachita.

Woganiziridwayo amawopa zotsatira za lamulo ndipo nthawi zambiri amawopa kutaya banja, okondedwa, nyumba, mbiri, udindo ndi ntchito. Adzadera nkhaâwa kuti ena angamunyoze.

MUTU WA CHIKHUMINDI CHITATU

MAU OMALIZA

Pamene ndimamaliza kulemba bukuli, ndinali ndi

mafayilo ambiri a atsikana amsinkhu yosiyanasiyana omwe adagwiridwa.

Yambiri mwa milanduyi inali ndi umboni wa nkhanza zogonana komanso nkhanza kwa ana m'Malawi. Milandu yambiriyi yomwe idachoka m'madera ndi m'mabanja imakhunkhadza kugonana pa chibale.

Anawa amachitiridwa nkhanza zogonana ndi abale awo, achibale chapatali, abwenzi a banja lawo, okhala moyandika-na nawo komanso owasamalira.

Nkhanza zochitika pogonana zikuchulukanso m'masukulu. Aphunzitsi amatenga udindo wawo m'kalasi pomwe ophunzira amagwiritsa ntchito kusankhana pakati pa amuna ndi akazi komanso kukakamizidwa ndi anzawo kuti achite zogonana posinthanitsa ndi zopindulitsa zakuthupi, kukhonza mayeso ndi kukonderedwa pa maphunziro monga kuthandizidwa m'maphunziro ovuta.

Zimanenedwa kuti kugwiririra ndi nkhanza zakugonana ndi zina mwa zifukwa zomwe zimachititsa kuti atsikana ambiri asamachite bwino m'maphunziro, azijomba komanso asiyire sukulu pa njira.

M'malo omwe umphawi ukukula m'banja, mwayi wa maphunziro ukuchepa, miyambo monga kulanda katundu wa masiye komanso komwe malamulo satsatidwa kwenikweni, ana kawirikawiri amayembekezedwa kuthandiza banja-lo kupeza ndalama. Izi ndi zoonza makamaka kwa atsikana, omwe kufunika kwawo m'mabanja ndi m'midzi kumaoneka kochepe kwambiri kuno ku Malawi.

Kupanda chidziwitso pa zomwe ana ogwira ntchito amakumana nazo komanso kusasamala za umoyo wa ana kuphatikiza umphawi wadzaoneni, kumapangitsa mabanja kutumiza ana awo ku ntchito zosayenera komanso zoopsa ndipo, pamapeto pake, amakachita uhule.

Kugwiritsa ntchito ana pa malonda ogonana ku Malawi kuno kumabwera ngati uhule wa ana m'madera, m'mizinda ikuluikulu ndi m'matauni kumene kukuchitika zokopa alendo komanso m'madera akumidzi. Atsikana ang'onoang'ono amagwiridwa m'midzi pofuna kupeza zinthu monga chakudya ndi zovala, makamaka pamene chuma chisakuyenda bwino.

Uhule wa ana umaonekera m'mizinda ikuluikulu ya ku Malawi ndipo umachitika kunja kwa malo omwera mowa usiku ndi m'malo ogona alendo kumene ogwiririra ndi amuna akumaloko.

Atsikana nthawi zambiri amakhala pa chiopsezo cha nkhanza zosiyanasiyana, kuzunzidwa komanso kugwiridwa.

Iwo akupitirizabe kuvutika ndi mitundu ingapo ya tsankho ndi kusalingana makamaka m'madera akumidzi. Pali miyambo ndi zikhaliidwe zingapo zomwe zimasokoneza atsikana.

Palinso kuchepa kwa kutenga nawo gawo kwa mwana wa mkazi m'maphunziro ndi moyo wapagulu. Zomwe zimapan-gitsa izi ndi zinthu monga kusalimbikira sukulu, kusachita bwino pa moyo, maphunziro otsika komanso kugonana ndi nkhanza zina m'sukulu.

Kuperewera kwa maphunziro kumapangitsa kuti atsikana aziziderera komanso kumalepheretsa mwana wa mkazi kukhala wodzidalira komanso kusankha yekha zochita. Izi zimathandizanso kuti atsikana asamatenge nawo mbali pa zochitika za pagulu ngakhale akakula. Maphunziro a mtsikana kawirikawiri samatengedwa ngati ndi ofunika ndipo amaperekedwa nsembe ku maukwati a ana.

Atsikana nawonso sakhala a thanzi la bwino komanso amanyetchera kusiyana ndi anyamata. Vutoli limakulanso chifukwa chosowa chithandizo cha uchembere wabwino. Atsikana ambiri amayamba kuchita zogonana adakali a ang'ono ndipo amakhala pa chiopsezo chotenga mimba, kuchotsa mimba, ndi kugwidwa ndi matenda opatsirana pogonana. Iwo amakumananso ndi mavuto okhudzana ndi kutenga mimba adakali a ang'ono, imfa za amayi oyembekezera, ku-sowa kwa chithandizo choberekera komanso kuchotsa mim-ba mosatetezeka.

Chiopsezo cha atsikana chawonjezeka ndi mliri wa HIV ndi Edzi. Ziwerengero zasonyeza kuti chiopsezo cha matendawa ndi cha chikulu pakati pa atsikana kuposa anyamata. Kupatula pazifukwa zomwe zanenedwa pamwambazi, mchitidwe komanso chikhulupiriro cha amuna akuluakulu

kuti kugonana ndi namwali kumachilitsa HIV ndi Edzi ukuyika atsikana pa chiopsezo.

Atsikana amakhala pa chiopsezo kwambiri akapezeka m'malo ena osatetezeka. Monga mwana wogwira ntchito, ndimakhulupirira kuti atsikanawa amazunzidwa ndi kugwiriridwa komanso amakhala ndi ntchito zolemetsa pakuti amaphatikiza ntchito za pakhomo ndi ku ntchito. Umboni umaonetsanso kuti pa ana okhala m'misewu, atsikana amagwiriridwa ndi anyamata anzawo komanso akuluakulu. Atsikanawa amathanso kuchita uhule akakhala mumsewu kuti apeze ndalama.

Mathero

MATANTAUZO AMAU

Kugonana ndi mwana wa mkazi: Uwu ndi mtundu wa nkhanza zogonana zomwe zimachitika pomwe munthu wag-onana ndi mwana wa mkazi yemwe sanakwanitse zaka 18 zakubadwa ku Malawi posatengera kuti anavomera kapena ayi malingana ndi Gawo 138 (1) la lamulo la Penal Code (Cap 7:01).

Kuchita zogonana ndi mwana: Izi ndi nkhanza zomwe zimachitikira kwa mwana wa m'muna kapena wa mkazi wochepera zaka 18 zakubadwa pomwe wayikidwa chiwalo cha umuna kukamwa kapena ku matako; kuseweretsedwa maliseche; kumboyu kapena mabere; kugwiritsidwa maliseche a munthu wa mkulu; kuzunzidwa m'thupi kapena m'maganizo pofuna kudzutsa chisangalalo cha kugonana ndi chisangalalo; ndi zonyansa zina zogonana malingana. Uwu ndi mu-landu malingana ndi magawo 160 A ndi B a lamulo la Penal Code.

Nkhanza zoonetsa mwana zolaula: Uwu ndi mtundu wa nkhanza wolola mwana kuti aone kapena aonere zolaula kapena oonetsa ana muzinthu zolaula komanso pogonana. Malingana ndi Gawo 160 D la lamulo la Penal Code, uwu ndi mulandu wo uonetsa, kugulitsa kapena kusonyeza zinthu zokhumudwitsa kwa mwana.

Nkhanza zogwiritsa ntchito ana pa malonda a uhule:

Izi zimachitika pogwiritsa ntchito ana kuti agone nawo posinthanitsa ndi ndalama kapena mphotho ina iliyonse. Mwanayo amatengedwa ngati chinthu chogonana nacho komanso malonda. Uwu ndi mulandu pa gawo 160 E la lamulo la Penal Code.

Kugonana pa chibale: Izi ndi nkhanza zomwe zimachitika pomwe anthu omwe ubale wawo uli pa magazi, ukwati, kapena polerana agonana monga kugonana kwa abambo ndi mwana wake wa mkazi; kapena amayi ndi mwana wake wa mwamuna; kapenanso mchimwene ndi mchemwali wake.

Kugwiridwa malo osayenera: Izi zimachitika pomwe mwana wagwiridwa malo osayenera mu njira zosiyanasiyana monga kulowetsa chinthu monga botolo kapena nthochi ku maliseche kwa mwana wa mkazi kapena kumbuyo kwa mwana wa m'muna; kulowetsa chiwalo cha umuna ku mbuyo kwana mwana; komanso kukakamiza mwana kuti agwire kapena ayamwe maliseche. Nkhanzazi ndi mulandu kutengera Gawo 137 ya lamulo la Penal Code.

Kuchitidwa chipongwe mwa kugonana: Nkhanzayi imachitika pomwe wina aonetsa zizindikiro zosonyeza zogonana kwa mwana. Izi zikapitirira ndipo mwanayo wanyasidwa nazo mwachidziwikire. Uwu ndi mulandu malingana ndi Gawo 6 la lamulo losawona kusiyana pakati pa akazi ndi amuna (Gender Equality Act).

One Stop Centre: Ndi malo omwe boma linakonza ndi cholinga chopereka thandizo kwa anthu omwe akukumana ndi nkhanza zogonana komanso kupereka uphungu kwa anthu omwe akhudzidwawo mwa zina. Malowa amapereka thandizo la chipatala (Kuyezedwa HIV, Kulandira PEP ndi

mankhwala oletsa kutenga mimba), uphungu komanso la polisi. Pali malo 28 oterewa mu dziko muno.

NJIRA ZOTETEZERA ANA KUNKHAZA ZOGONANA NDI KUGWIRIRIDWA



MAXWELL MATEWERE is a crime prevention expert who served as the Executive Director for Eye of the Child (www.eyeofthechild.org), a national organization recognized locally and internationally for its work in promoting the rights and general welfare of children in Malawi from 2008 to 2018. He is a well-trained and informed Child Rights Experts with depth of knowledge on Child Protection.

His keen analysis of child rights issues and challenges, and his creativity in using a multi-pronged strategy brought about visible changes in Malawi. Maxwell willingness to persist led to progress on various issues, including child justice, child care, child protection, end to child marriage, reduced cases of child trafficking, child labor, illegal inter-Country adoption, and institutionalization of children.

Maxwell made significant contributions to the development of child related projects and legislation regarding child protection, survival, care, support, and development in Malawi. Maxwell has spoken in front of both national and international audiences. He is always eager to learn from others and share what he knows. He is a systems thinker – always working to understand and find ways to impact the system while impacting the life of vulnerable children more deeply.

ISBN 978-99908-0-537-6



9 789990 805376